Munthu Woitanidwa Ndi Mulungu

. . .Neville. Ndi pepani basi kuti ndakusungani inu mutaima, mmbali mw a makoma. Ndipo ine ndinadutsa kuno pa chochita china, pafupi ora ndi theka lapitalo, ndipo anthu anali akubwerera pa chitseko, akumapita kwao. Ine ndinakomana ndi Billy kunja uko, ndipo iye anati malo anali atakonzeka kale kuti msonkhano uyambike, kuchokera madzulo ano. Chotero, ife tinangokhala nawo msonkhano waung'ono uwu kuno. Ife sitinawuyike nkomwe iwo mu mapepala akuno. Kotero, ife tingokhala ndi kanthawi kakang'ono ka chiyanjano.

2 Ndipo tsopano ndi zotangwanitsa nthawizonse, monga anthu a kunja kwa mzinda mungadziwe, kuti, kuno ku malo akwathu nthawizonse ndimakhalira kulumpha, kuthamanga kuchokera ku malo kupita ku malo, ndi kupanikizika. Chotero, ine ndikukhala ngati ndikuzolowera izo. Ine ndangofika pa malo amene ine sindikulola kuti izo zizindisautsa ine, mochuluka monga zikanathekera. Ndipo inu mukudziwa, iwe uyenera kutaya pang'ono pokha nthawi, ndipo iyenera kukhala yochuluka, ndi Ambuye. Ngati iwe suchita izo, ndiye iwe sumabwera mu msonkhano ndi kutsitsimuka kwa Mzimu Woyera. Ndipo pamene iwe ubwera mkati, monga lero zakhalira, pamene izo zangokhala chimodzi chachikulu, chokopa chachikulu, chabwino, izo zimakhala ngati zovuta nthawizina kuti ine ndibwere mkati, kuti ndipewe kukhala wotsinidwa pang'ono pokha ndi kukankha, inu mukuona, ndi kudzipangitsa ndekha kukwiya. Pamene ine ndichita izo, ndiye ine sindingakhoze kuupeza Mzimu Woyera paliponse mu izo.

3 Chotero, ine ndikumvera chisoni, ngakhale, kwa anthu amene aimirira mu—mu timipita ndi kuzungulira panja. Ndipo iwo amabwera, kuyang'ana mkati, kukalowa mu galimoto yawo ndi kumabwerera kwawo. Ine ndimafuna kuti nditenge sukulu yapamwamba kumusi kuno, kuti ndidzachititse msonkhano wa mausiku angapo okha, koma sukulu ikupitirira nthawi ino, ndipo ziri ngati zovuta kwa ine kuti ndiitenge iyo mu nthawi imeneyo. Koma ine ndikufuna kunena kuti inu ndikuyamikira ndithudi mmodzi aliyense wa inu, mkati muno ndi kunja, ndi chifukwa cha mgwirizano wanu wabwino, ndi pa zonse zimene inu mwachita.

4 Ndipo mmawa uno, mu Sande sukulu, ine ndinawathokoza anthu chifukwa cha chopereka chimene chinaperekedwa kwa ine usiku wathawu, chimene chinali chopereka chosapemphedwa.

Mosabisa, ine ndinawauza abusa kuno, abusa athu okondedwa, M'bale Neville, ndi iwo, ine ndikanakonda ngati iwo akanati asachite izo. Koma iwo anachita izo, chonchobe, chotero ine ndimangofuna kuti ndinene pa izo. Tsopano, ano ndi malo aang'ono, ndipo iwo sangati akhazike kupitirira pafupi anthu mazana atatu, ine sindikuganiza. Ndipo choperekacho chinali madola mazana atatu ndi makumi awiri mphambu anai, chimene chikutanthauza kuti inali pafupi dolla imodzi aliyense. Ndi chopereka chopambana chimene ine ndinayamba ndapatsidwapo mu moyo wanga, pa chiwerengero cha anthu. Kawirikawiri, icho chimakhala pafupi masenti makumi awiri ndi anai pa munthu, makumi awiri ndi asanu. Masenti makumi awiri ndi asanu ndi awiri ndi chopereka chachikulu, kwa munthu. Koma ichi chinali pafupi dolla pa aliyense. Ndipo ine ndithudi ndiri kuyamikira izo.

5 Ndipo mwina ine sindinathe kutenga, mmawa uno, kuti ndifotokoze kwa ena a inu. Ife tinapeza zakudya, bokosi la zakudya ziri pa masitepe, ndi zopereka zazing'ono zomwe zatumizidwa kwa ife. Mkazanga ndi ine tikukhumba kuti tifotokoze kuthokoza kwathu kwa inu anthu. Ndipo ine ndikutsimikiza mwakupambana kumene ife tikudziwira, zonse izo zikhale kwa Ufumu wa Mulungu.

6 Ndipo izo zimandipangitsa ine kumangomverera ngati ndikukhumba ine ndikanakhala nao malo aakulu kwambiri kumene ife tikanakhoza kumangopitirira kupita mtsogolo kwa nthawi yaitali ndi kutumikira kwa anthu. Koma ngakhale usikuuno, ukatha msonkhano, ine ndikuyenera kumapita. Chimene, ine sindikhoza kuchoka usikuuno, koma mmawa molawirira, kuti ndizipita.

7 Ine ndidzabwerera Loweruka lotsatira usiku. Kudzachoka Lamlungu mmawa, kachiwiri, waku Colorado. Ziri basi umodzi pambuyo pa umzake womwe, kumapita.

8 Ndiyeno msonkhano wanga wotsatira waku tsidya la nyanja ukubwera mu Januwale, kumene kuli ku Australia ndi New Zealand, ndi kudutsa uko. Tsopano, ine ndikufuna inu kuti mundipempherere ine. Ine ndithudi ndikukhumba mapemphero anu.

9 Ndiyeno ine ndikufuna kuti. . . tonse ife kuti tikhale oyamikira kwa Mulungu Wamphamvuzonse, Yemwe watichitira ife zinthu zazikulu choterezi mu msonkhano waung'ono uwu. Ine ndikukhulupirira, kwa chiwerengero cha nthawi, zakhala ziripo zochuluka zimene zakwaniritsidwa mu msonkhano uno kuposa msonkhano uliwonse umene ine ndinayamba ndachititsapo mu moyo wanga pa kachisi uyu. Ambuye akungowoneka kuti akutsegula madalitso.

10 Ine ndaganiza, mwina, pa msonkhano uno, kuti kuchokera mu masomphenya amene ine ndakhala nawo, kuti utumiki

wanga ukuti usinthidwe ukhale wabwinoko ndi utumiki waukulupo. Tsopano izo zingochitika motsimikiza basi monga inu anthu munamva mautumiki ena atatu awa akunenedweratu, kapena ena awiri awa. Umodzi uwu udzakhala basi monga chomwecho, kungoti wokulirapo. Koma usiku woyamba, ine ndinangowaitanira anthu kuno ku guwa, ndinapita molunjika basi ku kuzindikira zamumtima. Usiku wachiwiri, ine ndinawatengera iwo mu chipinda, ndinapita molunjika basi ku kuzindikira zamumtima. Ndipo mausiku awiri otsiriza, ndiye, ife timawabweretsa iwo kuno pa nsanja, molunjika basi ku kuzindikira zamumtima.

11 Koma kungoti ndinenepo zinthu zina, mtumiki wakhungu analandira kupenya kwake pa nsanja.

12 Ndipo asungwana awiri aang'ono, usiku watha, atakhala mu chikuku, ali ndi matenda amene palibe mmodzi yemwe akudziwa chimene iwo ali, palibe dokotala. Mapazi awo aakulu patali, ndipo zala zawo zakuphazi zikugwa, zala zakumanja zikugwapo, ndipo palibe chimene chikanachitidwa kwa iwo. Ndipo basi pamene Mzimu unali kudzoza, ine ndinapita apo, ndipo mu Dzina la Ambuye Yesu, ndinatemberera matenda amenewo, ndipo kunyamuka kuchoka mu chikuku iwo anapita. Ndipo mmawa uno, amayenda kuzungulira kuno ku kachisi, monga mwana wina aliyense, ndipo anabwera kuno ndipo anadzabatizidwa ndi ubatizo wa Chikhristu, pomwe pano mu dziwe, mmawa uno.

13 Pamene ine ndinali ndi maminiti angapo a kuwerenga, kanthawi kapitako, ndipo uko kunali abwenzi ena a ine, M'bale Hoover, mtumiki wochokera kumusi mu Kentucky, amangodutsa kuno ndipo anawasiyira mawu akazanga, kuti usiku watha pa kuyitana mzere, kunja mwa omvera, akazi amene anali opanda makadi aliwonse a pemphero kapena chirichonse, atangokhala panja uko akupemphera. Ndipo uko kunali mkazi mmodzi yemwe anali asanadye, ine ndayiwala kuti ndi motalika bwanji, chakudya; zophuka mu mimba yake, monse zitadzaza. Ndipo Ambuye anamuitana iye ndipo anamuchiza iye. Ndipo mmawa uno iye anawuka ndi kudya kadzutsa wamuyezo wabwino, ndipo ali pano penapake usikuuno.

14 Ndipo ena, anali akunena zokhudza izo, ndipo, o, nthawi siikanati, itilole, pa zinthu zomwe Ambuye wathu wachita. Chotero, kwa ife, izo zikutipatsa ife kulimbika kudziwa kuti izo zangokhala pafupi, chinachake chikukonzekera kuti chichitike, chachikulu.

15 Usiku watha, utatha msonkhano, utatha Uthenga, ine sindinayambe pa nthawi iliyonse ndawuwonapo Mzimu Woyera ukudzoza konse anthu mokula mulimonse kuposa momwe Iwo unachitira usiku watha. Ife tikuyembekezera ku kwina, usikuuno. Ndipo tsopano mundipempherere ine.

16 Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge ena a Mawu odalitsidwa a Mulungu. Ndipo ife tisanawerenge Mawu, tiyeni tingoyankhula kwa Iye, ndi mitu yathu yoweramitsidwa mphindi chabe.

17 Okondedwa Atate Akumwamba, ife tikubwera kwa Inu usikuuno, mwina otopa pang'ono chabe mu thupi, koma, o, momwe mizimu yathu ili yofewera! Zizindikiro za Mulungu wamoyo, kuti Iye ali ndi ife, ndipo akutidalitsa ife, ndipo akutipatsa ife chija chimene Iye analonjeza, mopitirira, mochuluka, pamwamba pa zonse zimene ife tingakhoze kuchita kapena kuganiza. Ndipo ngati ife tapeza chisomo pamaso Panu, kupyolera pokhulupirira pa Mwana Wanu, Ambuye Yesu, ife tikanapempha usikuuno kuti Inu mukanatichezera ife kachiwiri ndi magawo awiri a Mzimu Wanu. Mulole Iwo utsanuliridwe mu mphamvu yaikulu ndi miyezo pa munthu aliyense pano, kuti akhulupirire Uthenga ndi kulandira Mphamvu ya Mzimu Woyera mu miyoyo yawo. Pulumutsani iwo amene ali okhoza kupulumutsidwa usikuuno, Ambuye, ndipo achiritseni iwo amene ali okonzekera machiritso. Perekani izi, Ambuye.

18 Ndipo pamene ife tikuwawona anthu akukanikizira mkati, ataimirira mu makomo, mazana akubwerera ku tchalitchi chaching'onochi, izo zikutikumbutsa ife kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse. Kuti, mu masiku pamene Iye anatichezera ife kuno mu mawonekedwe a thupi, kukanikiza kunali kwakukulu kwambiri, iwo sankakhoza nkomwe kuti afike kwa Iye ndi munthu, ndipo anachita kumubweretsa iye kupyolera pa denga la nyumba. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti usikuuno, kuti mmodzi aliyense yemwe ati akanikizire kulowa mwa njira iyi adzakhoze kulipiridwa monga munthu uja anachitira.

19 Dalitsani Mawu Anu pamene ife tikuwawerenga Iwo. Ndipo mulole Iwo akhale Nyali, Kuwala ku mapazi athu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

20 [Wina akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi.] Ayi. Rosella Griffith? ["Inde."]

21 Zangonenedwa kumene kwa ine pomwe pano kuti msungwana yemwe ine ndinamuitana mmawa uja . . . chidakhwa yemwe anakhala ataitanidwa mu msonkhano ku Chicago. Iye anali yemwe anali atakhala mu chipinda pamene Mzimu Woyera unayankhula kwa iye ndipo anati iye anali chidakhwa. Ndipo madokotala aakulu asanu aku Chicago anali atamulephera iye. Othandiza Zidakhwa anali atamulephera iye. Ndipo iye anaitanidwa, ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Iye anachiritsidwa. Iye sanachite chibaba kuti amwe kuyambira pa nthawi imeneyo.

22 Ndipo dona wina wamng'ono uko mu khonde la pamwamba pamtunda pa iye, yemwe anali mzake wa iye, omwe iwo

ankakhala mu Mzinda wa Calumet. Ngati aliyense akudziwa kumene uko kuli, ndimo mmizere ya mmalire kumene kuli koyipa kuposa Paris, France, mitundu yonse ya zoipa zikuchitikako. Ndipo ndinamuuza iye kuti iye anali wogulitsa zozunguza ubongo, ndipo iye anali wovina ndi Fred Astaire. Ndipo bambo ake anayipidwa nazo izo. Koma iye anawuka ndipo anati, "Bambo, bamboyu akulondola ndendende." Iye tsopano wakwatiwa, msungwana wamng'ono, ndipo ali pa njira yake, kumapita ndi mwamuna wake, akulalikira Uthenga.

23 Rosella ndi wogwira ntchito yautumwi, kuchokera ku ndende iliyonse kutumikira ndi chirichonse chimene iye angakhoze kulowamo, kuwauza zidakhwa kuti chiripo chiyembekezo, ndipo ndicho mwa Khristu.

24 Iye wakhala wolemedwa mochuluka kwambiri chifukwa cha bambo ake; si kupitirira kuposa dzana, pa maminiti-khumi, kuyankhulana kwapadera. Msungwanayo wakhala wothandizira kwenikweni wa misonkhano, kwa zaka zinai kapena zisanu zapitazi. Zimene iye anandiuza ine, mu kulongosola kwakung'ono kwa maminiti khumi, panja ku ngolo, pa zoyankhulana, kumene anati, "M'bale Branham, chirichonse chimene inu muchita, ndine wolemedwa moyipa chifukwa cha bambo anga. Iwo amakukondani inu, koma iwo sakubwera basi kwa Khristu."

25 Ine ndinati, "Rosella, Mulungu akudziwa momwe angati achitire izo. Iye akudziwa momwe angamupangire iye kuti achite izo."

26 Ndipo tamva kuti tsopano iye wakwiriridwa pansi pa galimoto itasenza miyala ya laimu. Tiyeni ife timupempherere iye.

27 Ambuye, pa kamwa ya mwana wamkazi wokhulupirika uja, ndipo iwo akodwa pansi uko, mwakuti akhoza kufa pansi apo; Mulungu, perekani kuti iwo asatero, koma moyo wao uyang'ane mmwamba ndi kukumbukira kuti Inu ndinu Mulungu Yemwe mukhoza kuyankha pemphero pansi pa mulu wa miyala ya laimu; mofanana monga Inu munakhoza kuchitira mu mimba ya nsomba, kapena mu ng'anjo ndi moto, kapena mu khola ndi mikango. Inu mudakali yemweyo. Atulutseniko iwo, Ambuye, Mkhristu wotsukidwa. Ife tikudziwa kuti zinthu zonse zimachitira palimodzi kwa iwo amene akukondani Inu. Ndipo ife tikupemphera kuti ichi chikhale chimodzi cha zinthu zimenezo, pamene ife tikuzipereka izo kwa Inu, mu Dzina la Yesu. Ameni.

28 Mu kuwerenga kwa Mawu usikuuno, mu Bukhu la Mafumu Wachiwiri, ine ndikukhumba kuti ndiwerenge mu mutu wachiwiri, kwa mutu wapang'ono chabe, kuti ndipeze nkhani yake, Mulungu akalola.

Ndipo zinafika pochitika, kuti *pamene* Yehova *anati amutengere mmwamba Eliya* kupita *kumwamba mu*

kamvuluvulu, kuti Eliya anapita ndi Elisha kuchokera ku Giligala.

Ndipo Eliya anati kwa Elisha, Dikira iwe *pano, ine ndikukupempha iwe; pakuti* Yehova *wandituma ine ku Bet-eli. Ndipo* Eliya *anati kwa iye, monga* AMBUYE *alimoyo, ndi moyo wanu ulipo, ine sinditi ndikusiyeni inu. Chotero iwo anapita mpaka ku Bet-eli.*

Ndipo ana a aneneri . . . anali kumeneko *ku Bet-eli anabwera uko kwa Elisha, ndipo anati kwa iye, Kodi iwe ukudziwa kuti* Yehova *akuchotsera mbuye wako pa utsogoleri wako lero? Ndipo iye anati, Inde, ine ndikudziwa izo; khalani . . . muli chete.*

Ndipo Eliya anati kwa iye, Elisha, dikira pano, ine ndikukupempha iwe; pakuti Yehova *wandituma ine ku Yeriko. Ndipo iye anati, monga* Yehova *alimoyo, ndipo moyo wanu ulipo, ine sinditi ndikusiyeni inu. Chotero iwo* anapita *ku Yeriko.*

Ndipo ana a mneneri . . . *anali* uko *ku Yeriko anabwera kwa Elisha, ndipo anati kwa iye, Kodi ukudziwa iwe kuti* Yehova *akuchotsera mbuye wako pa utsogoleri wako lero? Ndipo iye anayankha, Inde, ine ndikudziwa izo; khalani . . . muli chete.*

Ndipo Eliya anati kwa iye, Dikira pano, *ine ndikukupempha iwe, pakuti* Yehova *wandituma ine ku Yordani. Ndipo iye anati, monga* AMBUYE *Alimoyo, . . . moyo wanu ulipo,* ine *sindikusiyani inu. Ndipo iwo awiri anapitirira.*

29 Ambuye atawonjezera madalitso Awo ku Mawu Ake. Phunziro langa la usikuuno ndilo: *Munthu Woitanidwa Ndi Mulungu.*

30 Ndipo ine ndiyesa kuti ndikhale mwachidule basi monga ndingakhoze, chifukwa ife tiri ndi mzere wa pemphero waukulu umene ukubwera mu maminiti pang'ono chabe, koma, kungoti ndikupatseni inu kuyang'ana kwakung'ono pa nthawi zimene ife tiri kukhalamo. Ife tikumva kulira uku pa wailesi, ndi mmalo osiyana, ndi kuchokera ku mitima yodzipereka, "Ambuye, tipatseni ife chitsitsimutso mu nthawi yathu." Ndipo kuchokera pa makalata ochokera kwa Akhristu kuzungulira dziko, ife tikumva kulira kumeneko, ndipo izo zimachita chinachake kwa mtima wako. Izo ndi zodzoza. Izo ndi zokunyamula. Izo ndi zofulumizitsa, kwa moyo, kumva anthu a Ambuye akuitanitsa chitsitsimutso. Ndipo Mulungu anapanga lonjezo, "Ngati anthu amene ali oitanidwa ndi Dzina Langa adzadzisonkhanitsa okha palimodzi ndi kupemphera, ndiye ine ndidzamva kuchokera Kumwamba." Ndipo chotero ife, usikuuno, tikufuna kuti tiganize pa izo. Ndipo kumbukirani, kuti, mkati mwa kulira konse uku, Mulungu sangakhoze kutumiza chitsitsimutso

mpaka Iye ali nawo amuna moyenera kuti achitenge icho. Ife sitingakhoze kukhala nacho chitsitsimutso mpaka ife titapeza amuna, amuna oyitanidwa ndi Mulungu, amuna ophunzitsidwa ndi Mulungu, omwe sali ophunzitsidwa mu sukulu za zamulungu ndi za maphunziro, koma amuna opirira a chikhulupiriro, omwe Mulungu wawalera mu sukulu ya kuphunzitsa Kwake kovuta. Amuna amene sali owopa kuti akumane ndi moto! Amuna amene abwerapo mu Kukhalapo kwa Mulungu; ndipo akudziwa mphamvu Yake, ndipo akudziwa umphamvuzonse Wake, ndipo akudziwa mphamvu Yake yochiritsa! Amuna ena amene aphunzitsidwa kuti amudziwe Mulungu wamoyo! Ndi zabwino kuwaphunzitsa iwo mwa Mawu, koma, "Lemba limapha; Mzimu umapatsa Moyo."

31 Ndipo ife tisanati tikhale nacho chitsitsimutso ichi, Mulungu ayenera kuti aitanepo ndi kuwaphunzitsa amuna, amuna ophunzitsidwa ndi Mulungu, kuti awutenge Uthenga uwu. Ndipo iwo samasamala kuti kutsutsako ndi chiyani. Iwo amakhala ali ololera kuti apite ku ng'anjo ya moto mwa kugonja, kapena ku makola a mikango, kapena kulikonse kumene kungakhale kuli. Iwo ali okonzeka kuti apite, chifukwa iwo akhala ali mu Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo akudziwa chomwe Iye ali. Kaya ndi ku chigonjetso kapena kugonja, iwo amaima apobe chimodzimodzi. Ndiwo mtundu wa kaphunzitsidwe kamene Mulungu amachita kwa anthu. Ndipo ndi chachilendo kwambiri kuganiza kuti Mulungu akanakhoza kuchita izo, kuti Mulungu amaphunzitsa amuna Ake monga choncho, koma Iye amatero. Inu mukudziwa, ife tiri nayo nyimbo yachikale imene timayimba:

> Ena kupyola mmadzi, ena kupyola mnamondwe,
>
> Ena kupyola mmayesero ozama, koma tonse kupyola mMwazi.

32 Mulungu amatsogolera anthu Ake kupyola mmayesero aakulu, kuti awatsuke iwo. Ndipo nthawizina izo zimatenga zaka kuti achite izo. Ndipo kwa inemwini, usikuuno, ine ndikukhulupirira kuti pakali pano Mulungu akuwaphunzitsa amuna oterowo kuti akakomane ndi mzere wapatsogolo, amuna amene akupyolamo, ndi, nthawi, kugwedezedwa kuchokera ku mapazi awo. Nthawizina zimawoneka ngati chinthu chonsecho chikugwa, komabe, mkati mwa izo zonse, iwo amamudziwa Mulungu wamoyo uyo ndipo amaika nkhope zawo patsogolo, kukhala akumasunthabe.

33 Ndipo anthu ambiri akupempherera chitsitsimutso, ine ndikudabwa ngati ali nthawizina, ngati iwo amene akupemphera, ngati mapemphero awo omwe samaimitsa zitsime za madalitso. Pamene, ali mwamantha ndi owopa kuti amudalire Mulungu, owopa kuti amutenge Iye pa Mawu Ake, owopa kuti

akhulupirire kuti Iye akadali wamoyo lero, pamene Baibulo Lake limanena mwachimvekere, kuti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

34 Mulungu samaitana, mwakamodzi, anthu anzeru, ophunzira, aluntha. Iwo amasewera gawo lawo, ndipo iwo ndi anthu opambana. Koma kawirikawiri pamene Mulungu afuna kuti ntchitoyo ichitidwe, Iye amatenga winawake yemwe sadziwa nkomwe ABC wake. Fufuzani Malemba. Penyani kupyola mmbirizakale. Amuna amene anafika ku chinachake ndi Mulungu sanali amuna omwe anali ndi maphunziro aakulu, koma amuna omwe, chabwino, anali opanda maphunziro, kukhumba kokha mu mtima mwawo kuti amutumikire Mulungu. Iye ankatenga mlimi, m’busa, nsodzi, msaki, iwo amene ankakhala mu chirengedwe. Mu kayeziyezi ndi kachetechete uja wa chirengedwe, uko Mulungu amakhoza kuyankhula kwa iwo. Ndipo ndi omwe Iye ankawaitana.

35 Ndipo ngati iwo apeza kuti, pamene Iye akupereka kuitana kwa waluntha wamkulu, munthu ameneyo potsiriza amabwerera ku malingaliro ake aluntha. Ndipo pakapita kanthawi, pamene izo zifika pakuti achite chopambana, iye amakhala ali wosokonezeka kwambiri ndi anthu a mdziko, kuti avomereze zoterozo. Chotero, iye amatsirizira ku chipembedzo, ndipo amapitirirabe kumbali ndi kukapanga mtumiki. Ndipo izo zonse nzabwino, ndipo ine ndiribe kanthu kotsutsa munthu ameneyo yemwe angati achite izo.

36 Koma pamene Mulungu akonzeka kuti achite chinachake mu malo auzimu, Iye kawirikawiri amatenga munthu yemwe Iye angakhoze kuika chidaliro Chake mmenemo, ndipo amamudzoza iye ndi kumutumiza iye kunja, ndipo iye ndi wopandamantha pa ntchitoyo. Ndiwo mtundu wa amuna amene ife tikuwasowa lero; osati masikolala opukutidwa, koma amuna amene amamudziwa Mulungu mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake.

37 Mwa chitsanzo, panali mwamuna mu Baibulo, dzina lake Mose, yemwe anali ndi kuphunzitsidwa kwake konse. Iye ankadziwa zamulungu zonse. Iye ankadziwa chirichonse chimene iye ankayenera kuti achidziwe. Ngakhale iye akanasowa maphunziro aliwonse, iye akanakhoza kuwaphunzitsa olamulira mu Israeli, kapena mu Igupto. Iye sankasowa chinthu chimodzi. Ndipo Baibulo limatiuza ife kuti iye anali wophunzira mu nzeru zonse za Aigupto. Mwakuti, iye ankakhoza kuwaphunzitsa masikolala awo. Iye ankakhoza kuwaphunzitsa azasayansi awo, zinthu. Iye anali ndi mafungulo mpaka ku nsonga yomwe, pamene izo zifika ku zaluntha. Koma, apobe, izo zinamutengera Mulungu zaka makumi anai kuti apunthe zonse izo zichoke mwa iye, kunja uko mu michenga. Ndipo pamene iye anapeza malingaliro ake onse aluntha a

Mulungu atapunthidwa kuwachotsa mwa iye, kunja kuja mu michenga, chitsulo chinali chokonzeka kuti chiwumbidwenso.

38 Umo ndi momwe Mulungu amawatenga anthu Ake ndi kupunthamo mantha awo onse ndi luntha lawo lonse, ndiyeno Mbuye Wowumba wamkulu amawaika iwo pa gudumu ndipo amayamba kuwawumbanso iwo kachiwiri. Amuna antchito, oyenera! Ndiye munthu wa Mulungu. Ndani yemwe angamuphunzitse munthu mochuluka kuposa Mulungu Mwiniwake? Penyani momwe Iye amawaphunzitsira iwo.

39 Ife tikanakhoza kulingalira kachiwiri za wina, dzina lake Davide. Mulungu anali kumuphunzitsa Davide pamene iye anali mnyamata wamng'ono chabe. Mneneri Samueli anabwera uko ndipo anatsanulira mafuta pa mutu wake, ndipo anamudzodza iye, chifukwa Mulungu ankafuna kuti amuphunzitse Davide kuti akhale wankhondo wamphamvu. Ndipo tayang'anani pa kuphunzitsa kumene Iye anamupatsa iye.

40 Ine ndinali kuwerenga, nthawiyina kale, kumtunda kuno ku Chigayo cha a Green, kumene ine kawirikawiri ndimapita kukapemphera, kumene Mulungu ananena kwa Davide, "Ine ndinakutenga iwe kuchokera ku khola la nkhosa, kuchokera kotsatira nkhosa zapang'ono zija za atate ako kunja kuja, ndipo Ine ndinakupangira iwe dzina lalikulu ngati amuna aakulu a pa dziko."

41 Ndipo ine ndikuganiza za kuphunzitsa kolimba kumene Iye anachita kwa Davide. Iye sanachite kumuphunzitsa iye mochuluka kwambiri mu sukulu ina, koma Iye anamuphunzitsa iye mu sukulu Yake yomwe. Davide anali msaki ndi wolishya. Ndipo mu Masalmo iye analemba za msipu wobiriwira ndi madzi odikha, chifukwa kumeneko iye anali ali yekha, kwa iyeyekha. Iye sanali atakhathamitsidwa ndi zinthu za mdziko.

42 Mulungu ayenera kumuchotsa munthu ku zinthu za mdziko, kuti Iye akhoze kumufikitsa iye mwachete, kuti iye azikhoza kumvetsera kwa Mulungu, ka Liwu ka kachetechete kaja, kakang'ono. Ndiye, kamodzi akakomana ndi Mulungu, iye amakhala wopanda mantha ndiye. Zindikirani kuti iye samasamala chimene aliyense anena; iye wakhala ali mu Kukhalapo kwa Mulungu. Iye akumudziwa Mulungu mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake.

43 Ndiyeno, Davide, ife tikumuwona iye. Tsiku lina, Mulungu analoleza chimbalangondo kuti chibwere ndi kudzatenga imodzi ya nkhosa zake. Davide anangopita motsatira chimbalangondo chimenecho. Mosakaika koma kuti iye anapemphera, chifukwa kanthawi kenako iye anavomereza za izo. Ndipo iye anapemphera ndipo anamupempha Mulungu. Iye anali wosamalira wa nkhosa imeneyo. Iye sakanakhoza kuitaya nkhosa imeneyo. Ndipo iye ayenera kuti aipulumutse nkhosa imeneyo, mwa mtengo wonse. Ndipo iye anatenga legeni yake

yaing'ono, ndipo anapita motsatira chimbalangondo chija ndipo anachipha icho. Iye ayenera kuipulumutsa nkhosa imeneyo. Inu mukuona chimene Mulungu anali kumuphunzitsira iye?

44 Mulungu akufuna kuti azibusa Ake azipulumutsa nkhosa, mosasamala chimene iye angati azitchedwa ndi zomwe iye ayenera kuti azidutsamo. Azipulumutsa nkhosa zimenezo!

45 Ndiye Iye anawona kuti Davide anali wolimba pa chimbalangondo ichi, kotero Iye anangokweza mphamvu ya chinyamacho mokulira pang'ono, ndipo Iye anatumiza mwanawankhosa . . . mkango unabweramo ndipo unadzatenga imodzi ya anaankhosa.

46 Ndipo mkango ndi chinyama chopandamantha. O, mu Afrika, pamene ine ndinali kusaka izo . . . Mkango ukhoza kupha amuna khumi iwe usanati, "Jack Robinson." O, chirombo champhamvu, chachikulu! Ndi kubangula kwakukulu kokha ndi, basi, anthu amadyedwa. Ndipo iwo amene amafa pansi pa mphamvu ya mkango samamverera kuwawa kulikonse. Ndi chowopsya chotero, kuti umve kubangula kumeneko pamene iwo ukupereka. Mapazi aakulu amphamvu awo, mu mphindi chabe, iye amagwetsera pansi amuna dazeni.

47 Ndipo kuti uganize, za mnyamata wamng'ono! Baibulo limati iye anali "khanda." Izo zikutanthauza kuti iye anali munthu wamng'ono chabe, ndi kugenda kwakung'ono kwa legeni. Inu mukudziwa chimene icho chiri, kachidutswa kakang'ono ka chikopa ndi chingwe ku mbali iliyonse. Ndipo mkango wanjala, uli nako kale kulawa kwa magazi mkamwa mwake, unathamangira umo ndipo anaimbwandira nkhosa. Davide anayang'ana mmwamba kwa Mulungu, ndipo anati, "Ine sindingakhoze kuitaya imeneyo. Inu mundithandize ine, Ambuye." Ndipo iye anaugwetsera mkango pansi, ndi kugenda kwa legeni. Ndipo pamene mkango unawuka momutsutsa iye, mnyamata wamng'ono ameneyo, ndipo mkango wolemera pafupi mapaundi mazana asanu, kapena bwinoko, mnyamata wamng'ono ameneyo akulemera mwina makumi asanu ndi awiri kapena makumi asanu ndi atatu. Iye anakoka, kuchokera ku lamba wake wamng'ono, mpeni. Ndipo pamene mkango unawuka, umene ukanapha amuna khumi mwa kukwapula kungapo, iye anawumbwandira mkango pa ndevu ndipo anawupha iwo.

48 Kulimbamtima! Mulungu samafuna amantha. Iye sangakhoze kukugwiritsa iwe ntchito ngati iwe ukuchita mantha kuti uwatenge Mawu Ake ndi kumukhulupirira Iye. Iye akufuna amuna olimba, osasamala chirichonse koma chimene Ambuye anena. Ndiwo mtundu umene Iye akufuna kuti aziyenda nawo. Mosasamala zimene mpingo unena, zimene m'busa anena, zimene mpingo uli kuimira; iye amaimira Mulungu ndi chilungamo, ndi Mawu Ake. Ndiwo amuna ife . . . Mulungu

awatumize masiku ano kwa chitsitsimutso Chake chimene anthu Ake akuchipempherera.

49 Kenako mu zaka, pamene iye anapita kuti akakomane ndi abale ake ku nkhondo, uko kunali chimphona china chachikulu kumtunda uko, zala mainchesi khumi ndi anai. Ndipo iye ankabwekerera, ndipo iye ankati, "Tsopano mloleni wina abwere adzamenyane ndi ine. Ngati inu mungakhoze kundikwapula ine, ine ndigonjera; ndi inunso momwemo, ndipo ife tidzatumikira." Yense yemwe ati agonjere, ndithudi, akhala iye yemwe ati agonje.

50 Ndi momwe Mdierekezi amakonda kuchitira izo. Pamene iye aganiza kuti iye wafika mmalire mwako, iye amakuuza iwe, "Iwe sungakhoze kumapitirira nazo izo. Iwe sungakhoze kulalikira machiritso Auzimu mu mpingo wa Methodisti, mpingo wa Baptisti." Chabwino, inu alaliki a Methodisti mudzangofika pomugwira Mulungu nthawi imodzi, ndipo mudzapeze ngati inu mungakhoze kapena ayi. U-nhu. Inu simudzakhoza konse kuchita izo ndi zamulungu zanu zimene iwo amaphunzitsa. Inu mudzasowa kuti mufike pomugwira Mulungu ndi kudziwa kuti Iye ali.

51 Iwo amati, "Anthu Achipentekoste." Zaka zingapo zapitazo, uko kunali gulu la anthu linkaima pa ngodya, opanda nkomwe—nyumba zimene iwo akanakhoza kulowamo. Koma kodi inu munawerenga mu *Life* magazini, tsiku lina, zomwe iwo ananena za iwo? Ndicho chimodzi cha zopambana zazikulu zomwe m'badwo uno unayamba wazidziwapo, ndicho kuwuka kwa mpingo wa Chipentekoste. Zedi. "Ndipo iwo amapanga otembenuka ochuluka mu chaka chimodzi kuposa momwe mipingo ina yonseyo ingachitire, itayikidwa palimodzi." Ndicho chimene *Life* magazini inanena. Bwanji? Iwo akhoza kukhala ali osokonezeka mu zinthu zina, koma, m'bale, iwo ndi olimbamtima; ataima kunja uko, chala-ku-chala, ndi kutcha chakuda "chakuda" ndi choyera "choyera." Pamene potsitiriza chitsitsimutso chiti chisweke, icho chiswekera pakati pa iwo. Inu mupenye ndi kuwona ngati izo sizitero. Iwo adzawongoledwa, limodzi la masiku awa.

52 Ndipo, Davide. Pamene Sauli anaika chida chake pa iye, ndipo anati, "Davide, ngati iwe uti upite kukamenyana naye munthu uyu, chimphona . . . " Anati, "Bwanji, sindiwe kanthu koma mnyamata, mwana chabe, ndipo iye wakhala ali wankhondo kuyambira ali mwana. Iwe ungakhoze bwanji kumenyana naye iye?"

53 Tamvetserani kwa Davide wamng'ono uyu. Inu mukuona, iye sananene izi monga chonchi, "Sauli, wolemekezeka inu, bwana. Bambo anga anandituma ine ku sukulu ya galamala, koleji, sukulu yapamwamba. Ine ndiri ndi Ph.D. Ine—ine—ine ndiri

nazo zida zoti ndichitire izi. Ndine munthu wophunzira." Iye sananene konse izo monga choncho.

54 Iye anati, "Mbuye wanga," iye anati, "pamene ine ndinali kuweta nkhosa za bambo anga kutsidya uko, chimbalangondo chinabwera ndipo chinadzatenga imodzi, ndipo ine ndinachipha icho. Ndipo mkango unabwera ndipo chinadzatenga imodzi, ndipo iye ndinaugwetsera iwo pansi. Ndipo pamene iwo unadzukapo, ine ndinawupha iwo." Ndipo iye anati, "Mulungu yemwe anandipulumutsa ine ku dzanja la chimbalangondo ndi mkango, akhozanso kundipulumutsa ine ku manja a Mfilisiti wosadulidwa uyo." Munthu wophunzitsidwa ndi Mulungu!

55 Apo anaima Sauli ndi kuphunzira konse kumene munthu aliyense angakhoze kukhala nako, kuti azidziwa momwe angamenyere. Davide sankadziwa kanthu za lupanga. Iye sankadziwa kanthu za chishango. Ndiye, Sauli anapita ndipo anakaika chida chake chachikulu champhamvu pa iye, ndipo Davide wamng'ono anali ataima wamatewe pafupifupi. Iwo anapeza kuti chovala chake chachipembedzo sichinamukwanire munthu wa Mulungu; zinangomugwetsera iye pansi. Ndipo tizikhulupiriro tathu tonse ndi zinthu sizingafanane konse ndi chida cha Mulungu kutsidya.

56 O, momwe ife tingakhoze kumangopitirira pitirira, ndi kunena zochuluka, za ochuluka ena osiyana. Koma, molunjika ku mutu wathu, kuti tifulumire.

57 Eliya anali kuyamba kukalamba, ndipo iye anadziwa kuti izo sizikanakhala ziri motalika kufika poti iye anayenera kuti achoke mdziko. Ndipo Mulungu anali atamupeza munthu yemwe anali munthu woonamtima, yemwe anali munthu wabwino. Dzina lake anali Elisha. Tsopano, ngati inu mutati muzindikire, mmodzi wa iwo dzina lake ndi Eliya ndipo mmodzi winayo ndi Elisha.

58 Tsopano, iye sanapite konse mu maonekedwe, ndi zina zotero, ndi kupita ndi kukapeza mu sukulu za zamulungu, ndi kupita ku sukulu zapamwamba zazikulu za masiku amenewo. Kodi iye anachita chiyani? Iye anapita kunja ku munda ndipo anakapeza munthu akulima ndi magori khumi ndi awiri a ng'ombe. Chiyani? Elisha, yemwe anali akulima, ankadziwa kuyamikira mzere woongoka. Ndipo iye ankadziwa kuti ngati iye akanati atembenuke ndi kuyang'ana mmbuyo, iye akanapotoza nasiya msewu. Ndipo Mulungu anadziwa kuti munthu yemwe amadziwa kulima mzere woongoka, amadziwa kuti asaike manja ake pa khasu ngakhale kupotoloka kuti ayang'ane mmbuyo. Iye sanayembekezere mpaka iye atapeza maphunziro ake, napotoza popitirira mu njirayo. Iye anangopha ng'ombe ndipo anapanga nsembe, ndipo ananyamuka kupita ndi Eliya, mwamsanga pamene chovala icho chinakhudza pa iye. Iye anali

wokonzeka, wololera. Mulungu ankadziwa kuti Iye akanakhoza kumupangitsa iye kukhoza.

59 Tsopano, Mulungu ayenera kuti amupatse iye maphunziro ena. Iye anakhala ali, kumuphunzitsa iye momwe akanati aziyika maso ake pa mzere, ndi magoli khumi ndi awiri a ng'ombe, ndi munthu mmodzi akulima ndi iwo. Iye anamuphunzitsa iye kupirira kwina, ndi momwe angakhalire wopirira, ndi kuziphunzitsa ng'ombe zija kuti ziziyenda mowongoka mu mzere.

60 Iye ankayenera kuti aphunzitse amuna ena, pambuyo pake; kuwayika iwo pa Baibulo, pa Mawu, atafola ndi Mulungu, kukhala moongoka mu mzere.

61 Ndipo, ndiye, ngakhale Mulungu anachita kumuphunzitsa iye pang'ono pokha. Iye anati, "Tsopano iwe udikire pano, pakuti ine ndikupita uko ku—ku Giligala. Ambuye andiyitana ine."

62 Ndipo mneneri, atamverera kale Mphamvu imeneyo pa iye, mwinjiro uja wa Eliya, iye anati, "Monga Ambuye ali wamoyo, ndipo solo yanu ili yamoyo, ine sindikusiyani inu."

63 Anapitirira mpaka ku Giligala, kumene kuli—malo a kuvomereza kwa Chikhristu ndi ubatizo. Ndiyeno iye anati, "Ingotsala pano tsopano. Izi ndi zabwino mokwanira. Iwe wapanga kuvomereza ndi ubatizo. Izi ndi zabwino mokwanira. Ine ndikupita mpaka ku *Beteli,"* kumene kumatanthauza, "nyumba ya Mulungu."

64 Tsopano izo zikanakhala zabwino kwa odzinenera ambiri. "O, ine ndangobwera kumene mu mpingo ndipo ndiri ndi chiyanjano. Bwanji osangokhala pomwe pano?"

65 Koma, mvetserani. Elisha sakanakhoza kuganiza mwanjira imeneyo. Iye anali atamverera kale Mphamvu ya Mulungu. Iye ankadziwa zinalipo zina kwa iye. Kotero iye anati, "Monga Ambuye ali wamoyo, ndipo moyo wanu ulipo, ine sindikusiyani inu." O, momwe ine ndikuzikondera izo!

66 Ndipo iye anapita mpaka ku Beteli, ku nyumba ya Mulungu, ndipo uko iye anakapeza gulu la masikolala. Iwo anali onse alaliki ophunzitsidwa bwino, ndipo iwo anayenda pozungulira ndipo anamuuza iye, anati. "Bwana, kodi inu mukudziwa chiyani? Inu muli pa mapeto aang'ono a ndodo. Kodi iwe umadziwa kuti Eliya amati atengedwe kwa iwe? Iye wakalamba kwambiri. Iye sangakhoze kukhala moyo motalika kwambiri. Eliya akuti atengedwe, ndipo iwe udzakhala utaima kunja uko monga wotentheka."

67 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake tsopano. Munthu yemwe anayamba wamulawapo Mulungu, sadzakhala ali wololera, kapena, sangakhoze kuthetsa ludzu lake pa chitsime chokumbidwa ndi munthu. Iye sangakhoze kuchita izo. Uko,

zamulungu zawo zonse zimene iwo anali nazo uko ku sukulu ya aneneri, sizikanakhoza kuthetsa ludzu la munthu wa Mulungu uyo, yemwe anali nako kulawa kwa Mulungu.

68 Ndipo iwo anapitirira kumukakamiza iye, "O, iwe uyenera kutsala pano. Ndipo, bwanji, mu masabata asanu ndi limodzi ife tikhoza kukupatsa iwe Ph.D yako. Ndipo iwe ukudziwa kuti izo sizikhala ziri motalika kwambiri mpaka iwe utatenga pafupi zaka zinai za kuphunzira kuno, ndipo ife tikhoza kukupatsa iwe ufulu woti uzilalikira. Iwe ukudziwa, ngati iwe usonyeza kuti ukuchita bwino, ife tikanadzakutumiza iwe mu chipembedzo chathu." Izo sizingakhoze kumukhutitsa munthu wa Mulungu. "Ife tikuphunzitsa iwe kuti ukhale mtumiki, ngati iwe uti ungokhala ndi ife pafupi zaka zinai kapena zisanu kuno."

69 Iye analibe nthawi ya zinthu za mtundu umenewo. Iye anali pa ulendo wake ku Kasupe uja. Iye anali atabwera pamwamba pa izo. Iye anali atalawa kale za Kumwamba mu solo yake.

70 Ndipo iye anati, "Kodi iwe ukudziwa kuti mtsogoleri wako akuti achotsedwepo?"

71 Ndipo mvetserani ku zimene iye ananena. "Inde, ine ndikudziwa izo. Koma khala bata lako." Mwa kuyankhula kwina, "Sungani mpweya wanu. Musati muyesere kundiuza ine za izo. Musati muyesere kundiuza ine zomwe ine ndikuchita. Ine ndikudziwa kumene ine ndikupita ndi chimene ine ndikutsatira." [M'bale Branham akuwombetsa manja ake katatu—Mkonzi.]

72 Mulungu, tipatseni ife amuna onga amenewo, amuna ophunzitsidwa ndi Mulungu amene sadziwa za kupotokera kumbali ku *izi* ndi kupotokera kumbali ku *izo*.

73 "Ine ndikudziwa kumene ine ndikupita. Ndipo musati muyankhule kwa ine za izo. Ingosungani mpweya wanu. Musati muyesere kundikhumudwitsa ine, chifukwa izo siziti zichite ubwino uliwonse."

74 O, ngati anthu amene apemphereredwa akanati angokhala ndi kulimbamtima kochuluka chotero!

75 "O, masiku a zozizwitsa anapita. Izo sizinali zenizeni. Inu mupenye, inu mukhala odwala kachiwiri."

76 "Ingosungani mpweya wanu. Musati mundiuze ine kalikonse ka izo. Ine ndikusuntha mopitirira. Chitsitsimutso chiri kudza. Mulungu wachilonjeza icho." O, inu ana aamuna a Mulungu, sunthirani kunja mu danga ilo kutali, opandamantha. Opandamantha! Mtengeni Mulungu pa Mawu Ake.

77 "Ine ndikudziwa iye—iye akuti akatengedwe achokepo. Koma izo siziri zimene ine. . . Inu mulibe chinthu pano choti chingandisangalatse ine. Madigirii anu onse ndi ma Ph.D, ndi Bachala ya Luso, ndi zinthu zonse izi, siziri kundikhutitsa ine. Ingosungani mpweya wanu."

"Chabwino, inu mukasweka kunja uko."

78 "Chabwino, ngati ine nditi ndisweke, ndisiyeni ine ndisweke. Ine ndiri pa ulendo wanga." Ulendo, iye anali akupita.

"Inu simungakhoze kuzipangitsa izo kuoloka."

79 "Ine ndikudziwa ine sindingakhoze kuzipangitsa izo kuoloka, koma Mulungu akandiwolotsa ine," iye anatero.

"Chabwino, Elisha akupita ku Yordani."

"Ine ndikupita ndi iye."

Mulungu akufuna Yordani mu moyo uliwonse.

80 Kotero, Elisha anabwera pamenepo. Anati, "Tsopano, Elisha . . ." Eliya ananena kwa Elisha, "Ndiwe munthu wamng'ono chabe," mwinamwake chinachake monga ichi, "ndipo kwenikweni inu simunakhale nako kuphunzira kulikonse." Mneneri wachikulireyo anali kuyesera kuti amuyese iye. Iye anati, "Ndiwe mwamuna wamng'ono chabe. Iwe sunakhale nako kuphunzira kokwanira. Bwanji, inu simuli . . . Ndi, kwenikweni, iwe sunakhale nawo maphunziro a sukulu ya galamala. Chinthu chokha chimene iwe umachidziwa ndi momwe ungalimire. Chotero iwe kuli bwino utsalire pano, ndipo ukhoza kupeza Bachala ya Luso yako. Mukuona? Iwe ndibwino utsalire kuti upeze digirii yako."

81 Koma osati Elisha, osati munthu uja yemwe anamukhudzapo Mulungu kamodzi, anamverera Mphamvu ija ya kudzoza pa iye. Iye anati, "Monga Ambuye ali moyo, ndi moyo wanu usanafe konse, ine sinditi ndikusiyeni inu." Iye anali ndi cholinga. Iye anawona masomphenya. Iye ankadziwa zimene zimati zikachitike.

82 Ndipo iwo onse anapita mpaka ku Yordani. *Yordani* amatanthauza "imfa." Uko iwo anaima, mwamuna wokalamba ndi mnyamata. Izo kwenikweni zikuimira Khristu ndi Mpingo Wake. Ndipo apo iwo anaima, mphepete mwa Yordani. Uko iye ali, akutsika kuchokera ku mapiri a Yudea, mafunde aakulu akukukuma monga choncho. Ndipo Elisha . . . ndi tsitsi lake laimvi logwera pansi kunsana kwake, ndi maso ake osawona bwino okalamba akuyang'ana kutsidya kwa Yordani. Ndipo mwamuna wamng'onoyo akupenyetsetsa kusuntha kulikonse kumene iye ankapanga. Mmodzi, mwamuna wamng'onoyo, anali akuyembekezera masomphenya, kuti achite chifuniro cha Mulungu. Mmodzi winayo anali akupita Kwawo. Iwo onsewo anali pa Yordani. Elisha, kwa iye . . . Iye akupita Kwawo.

83 Eliya anakhala moyo wovuta. Mlaliki wamkazi uja kumusi kuja anali atamupatsa iye nthawi yovuta yoti ayendemo, Yezebeli ndi Ahabu. Ndi miyala ndi zonse zimene iye anadutsamo! Elisha anali kuyamba kutopa. Ndipo iye ankadziwa kuti iye anali atamenya nkhondo yabwino, ndipo

iye anali atatsiriza mtundawo. Patsidya pa Yordani pokhapo nkomwe kunali kupuma ntchito kwake.

Koma Elisha anali akuyembekezera Mzimu uwo umene unali pa iye.

84 Kotero, ngati inu mutazindikira, wokhulupirira aliyense, pamene iwe ufika pa malo pamene iwe uyenera kuti ugulitse zonse, iwe udzamverera mafunde ozizira a Yordani akukuta pa mapazi ako. Kodi iwe uwoloka, kapena sutero? *Yordani* ndi "kulekanitsa," kulekana.

85 Ndipo ataima mmbuyo pa phiri anali alaliki awa, apobe, akukuwa pa Elisha, "Iwe kunali bwino kuti usawoloke. Iwe upitirira malire." Inu mumazimva izo, ndemanga, ngakhale, lero.

86 Koma, Elisha anati, "Ngati Mulungu ali Mulungu, ndipo uyo ndi mneneri Wake, ine ndiyenera kuti nditenge malo ake. Ndipo ine ndikusowa Mzimu Wake kuti ndichitire izo nawo. Ine sindikusowa sukulu yawo. Ngati sukulu yawo ikanakhala itachita izo, iwo akanakhala akutenga malo ake. Koma Mulungu anandiitana ine kuti ndizichite izo, ndipo ine ndikusowa Mzimu Wake."

87 Ngati masukulu a mipingo akanati atenge malowo, ndi Mphamvu imene Yesu anapereka, iwo akanazitenga izo, zaka zapitazo; Methodisti, Baptisti, Katolika, Presbateria. Koma iyo sidzachita konse izo.

88 Zimatengera Mzimu wa Yesu Khristu! Ndipo inu mudzawoloka Yordani, ya chipembedzo chirichonse kuseri kwa icho, china chirichonse, ndi kuima wekha ndi Mulungu.

89 Chotero, Iye anaima ndi iye pa Yordani. Elisha akuyang'ana mmwamba uko, akudziwa, kwinakwake kutsidya uko, Mulungu akanati akakomane naye iye. Ndipo iye anauvula mwinjiro wake, ndipo iye anayang'ana mozungulira kwa mwamuna wamng'onoyo. Ndipo iye anakantha Yordani. Ndipo pamene iye anatero, Yordani anatseguka. Ndipo iwo anayenda mowoloka, pa nthaka yowuma.

90 Mukuona, Yordani sali woyipa kwambiri, pambuyo pa zonse, ngati iwe uli nacho Chinachake limodzi nawe choti utsegulire njira.

91 O, pamene iwo anakagunda mbali inayo! Atakolowekedwa ku thengo lirilonse anali kavalo ndi galeta. Mfumu ya mafumu anali atatumiza operekeza kuti amubweretse Eliya Kwawo. Izo zonse zinali zitatha, kwa Eliya. Iye anali atakhala nazo zomkwanira za izo, pafupi zaka makumi asanu ndi atatu ndi chinachake, za kukangana ndi anthu awo kumeneko, ndi kumakhala ali . . . kudutsa mu njala ndi zokangana, ndi chinthu chirichonse. Iye anali wokonzeka kuti azipita Kwawo. Ndipo iye anayang'ana pamenepo kwa Elisha.

92 Ndipo Elisha ankafuna kuti awone masomphenya. O, iye anali ndi kuphunzira konse, kumbuyo kuja iye akanakhoza kuimako. Iwo sanali kufika kulikonse. Mulungu ankati amuphunzitse iye mwa njira Yake yomwe. Chotero pamene iye anayang'ana cha kumeneko, anayang'ana, konse—mathengo onse awo uko, atakolowekedwa pa magaleta awa a Moto ndi akavalo a Moto, izo zinachita chinachake kwa Elisha. Iye anawona masomphenya. Inde, m'bale!

93 Ndipo pamene Mulungu anamutengera Eliya mmwamba, iye anabwerera ndi magawo awiri a Mzimu wake. Iye anali wokonzekera chitsitsimutso pamenepo.

94 Zindikirani mwamunayo ndiye, pokhala mnyamata wolima chabe poyamba. Mulungu anapanga dzina lake kukhala lachisavundi. Aneneri onse amene anaima pozungulira, akumuyang'ana iye, anachita kugwada pa mapazi ake chifukwa iye anali nayo Mphamvu ya Mulungu pa iye. [M'bale Branham agogoda pa guwa katatu—Mkonzi.]

95 Liri kudza ora pamene Mulungu ati adzapange dziko kugwada pa mapazi a amuna ndi aakazi amene agweramo nadutsa ndipo awoloka Yordani, ndipo alekanitsa chinthu icho . . . okha, kuchoka ku zinthu za mdziko. M'bale ndi mlongo, usikuuno, chirichonse chimene muchita, chirichonse chimene mukuganiza, inu muwoloke Yordani ndi Mulungu. Pitirirani kuoloka ndipo mudzilekanitse, lisiyeni dziko mmbuyo. Muloleni Mulungu akuphunzitseni inu kwa utumiki Wake womwe. Ife tiri kukhala mu tsiku chisanafike chitsitsimutso chimenechi, koma Mulungu akufufuza, kuyesera kuti apeze mitima.

96 Penyani. Iye anamupeza mwamuna dzina lake Paulo, o, Mfarisi wochita zayekha. Koma Iye anachita kumugwiritsa iye ntchito, ngati, iye asanafike pokhala wophunzira. Penyani zimene Iye anachita, monse kupyola mibadwo, kwa anthu. Iye ankachita kuwatenga iwo ndi kupopera panja zamulungu zawo kuzichotsa mwa iwo. Ndipo Paulo, mwamsanga pamene iye anawona masomphenya, iye sanapite uko ku Yerusalemu, kwa Gamalieli, mphunzitsi wamkulu, wamkulu kwambiri mu Israeli, yemwe iye anaphunzitsidwa naye. Iye sanabwerere konse mmbuyo kwa iye, kuti akamufunse iye. Bwanji, iye sanapite nkomwe ku Yerusalemu, kwa zaka khumi ndi zinai zotsatira. Koma iye anapita uko ku Igupto, ku msonkhano wapemphero. Uko Mulungu anamulola iye kulemba Mabuku ochuluka a Chipangano Chatsopano. Mukuona? Mulungu akufuna amuna. Iye anali naye winawake yemwe Iye ankafuna kuti alembe Chipangano chimenecho, kotero Iye anangomusankha Paulo. Ndipo Iye anangomuchotsera zamulungu zake zonse mwa iye. Ndipo Paulo anati iye anachita kuyiwala zonse zimene iye anayamba wazidziwapo, kuti aphunzire Khristu.

97 Mulungu lero akuyesera kuti akhuthule dziko lichoke mwa ife, ndi kutitenga ife kuti tidzikhuthule tokha, ndi kukhala amuna ndi akazi opandamantha amene amamukonda Mulungu, ndipo akhala ndi Mulungu, ndipo awoloka mzere wolekanitsa, Yordani, kuti Iye angakhoze kutigwiritsa ife ntchito kwa ulemerero Wake.

98 Ili ndi ora limene ine ndikufuna inu kuti muganize molimba. Ndipo ngati inu simunayambe mwawoloka konse malo awa, ngati inu simunayambe mwafika powoloka mzere uwu, kumene inu mukanali kumati, "Chabwino, mayi anga anali a mpingo winawake." Izo zonse nzabwino. Izo sizimatenga malo anu. Mwaona?

99 Mulungu akuitanira amuna ndi akazi, lero, kutsogolo kwa nkhondo. Iye sikuti akuwaitanira iwo ku Giligala, ngakhale kuti Iye akuwaitanira iwo ku Yeriko, kapena Beteli. Iye ali . . . Awo adzawonongeka. Koma Iye akuwaitanira iwo kuti awoloke Yordani, kotero Iye angakhoze kukutengerani inu ku sukulu ya Mphamvu Zake Zomwe, ndi kukupangani inu ndi kukuwumbani inu.

100 Penyani zimene Iye akuchita komwe kuno tsopano, akutumiza pansi Mzimu wa Mwana Wake. Iye akuchita zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa, zimene dziko silinaziwone zaka zikwi ziwiri zapitazi. Dziko lasayansi lagwira chithunzi Chake, Lawi la Moto, Mngelo wa Ambuye. Lapachikidwa mu Washington, D.C., usikuuno, cha mu holo ya luso lachipembedzo, Chinthu chauzimu chokha chimene chinayamba chatsimikiziridwirapo mwasayansi kuti chinali chitajambulidwa. Iye akuyika apo zizindikiro Zake zomwezo ndi zodabwitsa.

101 Ndi chiyani icho? Ndiko kuwoloka Yordani. Kukhala wekha ndi Mulungu. Kugona mu ng'anjo Yake Yomwe yokonzedweramo. Kukhala pa gudumu lalikulu la Wowumba ndi kumulola Iye akuwumbe iwe. Usikuuno, pamene ife tiri mu pemphero, pamene ife tikufika ku malo amenewo, dzigonekeni nokha pa gudumu Lake lomwe, ndi kuti, "Ambuye, ine ndiri pano. Ndiumbeni ine ndipo mundipange ine monga mwa mapangidwe Anu Omwe." Ndipo Mulungu azichita izo.

102 Pamene, ife tikuweramitsa mitu yathu mphindi chabe kwa mawu a pemphero. Tisanati tipereke pemphero, ine ndikanafuna kuti ndifunse funso ili kwa anthu mkatimu ndi kunja. Ndi angati mkati muno moonamtima akanafuna kuti apite ndi Yesu mpaka ku Yordani, usikuuno, ndipo uko kukawoloka uko kumene inu mungakakhoze kuwona masomphenya ndi kukawona chimene Mulungu amatanthauza kwenikweni? Mungakweze manja anu? Mulungu akudalitseni inu. Tangoonani! Ine ndikungoganiza kuti alipo manja mazana awiri mnyumba muno, akwezedwa. Pitani

mpaka ku Yordani, osati mpaka ku seminare. Elisha anadutsa kumene cha pamenepo.

Iwo anati, "Dikira pano."

103 Iye anati, "Ine sindikufuna kutero. Izo ndi zopangidwa ndi anthu." Aa, izo sizidzakhoza kuthetsa nkomwe ludzu ilo la munthu yemwe akuchitira ludzu kwa Mulungu. Wopanda kujayira kwa ku seminare, wopanda—wopanda luso la madigirii, kapena zina zotero, sizidzakhoza, konse kuthetsa ludzu ilo, mpaka inu mutamwa kuchokera ku Kasupe wa Moyo uyo.

Inu amene munakweza manja anu, pempherani ndi ine tsopano.

104 Mulungu wokondedwa, mu maminiti pang'ono awa a utumiki, amuna ndi akazi ayima kuzungulira makoma, anyamata ndi asungwana; ndi panjapo, atatsamira pa mazenera; kotentha. Komabe pali chinachake mwa iwo, chimene Inu mwagwira tcheru chawo, kapena iwo akanachoka nkumapita. Iwo sakanati ayime pamenepo monga choncho.

105 Koma, Ambuye Mulungu, chifukwa iwo akudziwa kuti iwo ndi anthu okhalapo chabe. Ndipo ife tinawerenga mu pepala kumene mmodzi wa mameya athu akale olemekezeka amamvetsera kwa Purezidenti-Wachiwiri akuyankhula, anatengedwa napita. Wina ku masewera a mpira, usiku wina, mwamuna wodziwika, anapita mwamsanga. Ndipo miyoyo yawo ili kwinakwake usikuuno. Mulungu, imeneyo idzakhala njira yathu tsiku lina. Mwinamwake osati mwa chikhalidwe chofanana, koma ife tiyenera kupita.

106 Ndipo lolani amuna abwere kwa iwoeni ndipo azindikire kuti kungokhala wa mpingo si zimene Inu mumafuna. Inu mukufuna anthu kuti akhale odzazidwa ndi Mzimu, obadwa, otemedwa nkuchotsedwapo, owotchedwa mkati ndi Mzimu Woyera, odindidwa, anthu amene awoloka mzere, anthu oitanidwa ndi Mulungu. Ndipo ife tikukhulupirira kuti Inu mutumiza chitsitsimutso chimene Billy Graham ndi ena ambiri ali kuchipempherera. Pamene Inu mungakhoze kuwatengera anthu kwa iwowokha, kuchoka ku sukulu zawo za zamulungu, kuchoka ku njira za-kachitidwe kawokawo, anthu opanda mantha, anthu a—a khalidwe ndi Inu, amene amakukhulupirirani Inu ndipo amakutengani Inu pa Mawu Anu.

107 Mulungu, mulole ambiri a iwo ayime alipo tsopano, amene ati apereke zonse zimene iwo ali nazo kwa Ambuye Yesu, ndi kudzigulitsa mochoka ku dziko, kupita kupitirira Giligala, malo a kuvomereza ndi kuyamba kwa Chikhristu. Apite kudutsa sukulu ya aneneri imene inali kumbuyo kuja ndi zamulungu zawo. Apitirira mpaka ku Yordani, ku masomphenya otseguka pamene iwo anawoloka, akapeze kuti Mulungu wamoyo akanali wamoyo.

108 Kenako ife tikumupeza mneneri uyu akuyang'ana ponse pomzungulira iye, ndipo apo panali Angelo omwewa a Moto, ndi magaleta, ku Dothani kuja, tsiku lina.

109 Iwo akadali pano usikuuno, Ambuye. Itanani amuna Anu, itanani Akazi anu, anyamata Anu, asungwana Anu, Ambuye. Yankhulani mtendere kwa mitima yawo ndipo aloleni iwo kuti awolokere kwina kutali ndi zinthu za mdziko. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu ndi chifukwa cha Iye. Ameni.

110 Ine ndikufuna kuti ndiyimbe ijayi mphindi chabe, mwachete kwenikweni mwa kupembedza.

Khalani ndi njira Yanu, Ambuye!
Khalani ndi njira Yanu!
Gwirani chomwe ndiri
Mnjira ya mtheradi!
Ndiumbeni ndipangeni
Mwa kufuna Kwanu,
Pamene ndiyembekeza,
Wodzipereka mwa chete.

Tonse palimodzi tsopano, mwa njira ya kupembedza.

Khalani ndi njira Yanu,

Tsopano dziperekeni nokha ku nyimbo imeneyo, ndi nyimbo imeneyo, kwa Mulungu.

Khalani ndi njira Yanu!
Gwirani chomwe ndiri
Mnjira ya mtheradi!
Ndiumbeni ndipangeni
Mwa kufuna Kwanu,
Pamene ndiyembekeza,
Wodzipereka mwa chete.

111 Mwachete tsopano, mwa kupembedza tsopano. Musati muziyang'ana pozungulira. Ingoyang'anani kwa Mulungu.

Khalani ndi njira Yanu, (Tanthauzani izo kwenikweni.)
Khalani ndi njira Yanu!
Ndinu Wowumba;
Ndine dongo.
Ndiumbeni ndipangeni
Mwa kufuna Kwanu,
Pamene ndiyembekeza,
Wodzipereka mwa chete.

112 Ine ndikukhulupirira kuti izo zikanakhala zabwino kwenikweni. Inu mumakukonda kupembedza? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Uthenga watha tsopano. Tiyeni tizingopembedza, miniti, ndi mitu yathu itaweramitsidwa, nyimbo iyo kachiwiri. Tanthauzani izo kuchokera mu mtima wanu.

Khalani ndi Yanu . . .
Khalani ndi njira Yanu!
Ndinu Wowumba;
Ndine dongo,
Ndiumbeni ndipangeni
Mwa kufuna Kwanu,
Pamene ndiyembekeza,
Wodzipereka mwa chete.

113 Ambuye, perekani izi. Mulole mmodzi aliyense, kuchokera pa ana aang'ono awa mpaka kwa mwamuna wamkulu kwambiri ndi mkazi mu Kukhalapo Kwauzimu, mulole Mzimu Woyera pakali pano ugwire ntchito pa chikhulupiriro chawo ndipo uchotsepo kukaikira kwawo konse, kulephera kwawo konse kwakung'ono, ndipo mulole iwo kuti awumbidwe monga mwa chifuniro Chanu. Pamene iwo ali pa gudumu Lanu lalikulu la kuwumbira, ife tikugoneka miyoyo yathu kuti idalitsidwe, iwumbidwenso. Perekani izo, O Mulungu, mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu. Ameni.

114 Ine ndikungozikonda izi. Sichoncho inu? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mwachete kokha kumamverera Mzimu Woyera. O, utatha Uthenga wolimba, ndiyeno kukoma kuja kwa Mzimu Woyera! Iwo umabwera ndi Mawu. Ine ndikuti ndiyimbe ndime ya iyo, kapena kuiyesa iyo.

Ukuwukha magazi, inde, ukuwukha magazi,
Uthenga wa Mzimu Woyera, ukuwukha magazi,
Magazi a ophunzira ofera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera Ulikuwukha magazi.

Woyamba kufera dongosolo la Mzimu Woyera,
Anali Yohane M'batizi, anafa monga munthu;
Ndiye anadza Ambuye Yesu, anampachika Iye,
Analalikira kuti Mzimu udzapulumutsa anthu.

Kunali Petro ndi Paulo, ndi Yohane waumulungu,
Anapereka miyoyo kuti Uthenga uwu uwale;
Anasakaniza magazi, monga aneneri akale,
Kuti Mawu owona a Mulungu anenedwe moona.
Ndiye anamugenda Stefano, anatsutsa tchimo,
Anawakwiyitsa iwo, anamuphwanya mutu;
Koma anafa mu Mzimu, napereka mzimu,
Anapita kwa enawo, opereka moyo.

Miyoyo pansi pa guwa, ikulira, "Mpaka liti?"
Kuti Ambuye alange ochita zoyipa;

Koma kukhalanso ena opereka magazi
Kwa Uthenga wa Mzimu Woyera ndi mtsinje
Wake wofiira.

Tonse limodzi tsopano.

Ukuwukha magazi, inde, ukuwukha magazi,
Uthenga wa Mzimu Woyera, Ulikuwukha
magazi,
Magazi a ophunzira ofera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera Ulikuwukha
magazi.

115 Kodi iwo anali ndani? Amuna amene Mulungu anawaphunzitsa ndipo anawaitana. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Angakhoze bwanji Mulungu kumugwiritsa ntchito wamantha kuti aike Mawu ake mmenemo? Iye ndi woopa. Ndicho chifukwa iwo sakudziwa kanthu za Iwo. Amuna amene sali owopa, amene Mulungu wawadula ndi Mzimu Woyera, Mulungu akukhala mkatimo. Iye akanangoti asindikize mwamsanga magazi ake ngati panalibe, umboni wake ndi magazi ake; samafuna kusamala. Ndi Khristu yemwe akumukhalira moyo. "Pakuti ine kuti ndikhale moyo ndi Khristu, ndipo kuti ndife ndi phindu." Ndi momwe iwo ankamverera za izo. Ameni.

116 Tsopano ndi nthawi ya mzere wa pemphero. Ndipo ndi mzere wa pemphero wolawirira, pafupi twente pasiti eyiti. itapitirira 8.00. Koma ife tikufuna kuti tiwapempherere anthu. Ndipo ine ndikufuna inu tsopano, ichi . . . Kulalikira konse kumene ife tikanakhoza kuchita sikukanati—osati ufanizitse ndi Mawu amodzi oyankhulidwa ochokera kwa Mulungu Mwiniwake.

117 Tsopano kuti tiyambe mzere wa pemphero, umene, ife tinalonjeza kuti tiwapempherere onse. Icho ife tichita, Mulungu akalola. Ife, usiku uliwonse, takhala tikupereka makadi a pemphero. Ndi kunena, mu izi, kuti . . . Usiku uliwonse ife tikuyitana gulu kuchokera apo, ku kuzindikira za mumtima. Koma anthu, ndiye, ena a iwo adzakhala akuchoka usiku umenewo. Ife tikanakhala ndi msonkhano wawukulu, ndipo Mzimu ukanati uzigwa, ndipo anthu akanati azichoka. Ndipo usiku wotsatira ife tikanati tiperekepo owonjezera.

118 Ndipo ngati ine sindiri kulakwitsa, kodi ine sindiri kuyang'ana pa Fannie Wilson ataima kumbuyo uko? [Mlongo Wilson ati, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.] Ine ndikukumbukira ndikumutenga mkazi uyo, pafupi khumi ndi zisanu ndi ziwiri . . . O, kupitirira apo pafupi makumi awiri- . . . ["1932."] 1932, akufa, ndi TB, ndipo dotolo wa mzinda uno anali atamulephera iye. Ndipo iye anali akutaya magazi mpaka mabulangeti ndi chirichonse zinali kukhala zitanyowa ndi magazi. Mwamuna wake ndi mwana wake wamkazi anabwera ndipo anadzanditenga ine, mmawa wina. Tinapita kumeneko

ndipo tinakaitanira pa iye, Dzina la Ambuye Yesu. Ndipo pafupi masiku angapo kenako, mu nthawi yozizira ya chirimwe, ine ndinamubatiza iye mu Dzina la Ambuye Yesu, ku mtsinje. Ndipo iye anabwera ndi msewu, kumbuyo kwa ngolo yachikale ya ng'ombe, wonyowa momwe iye akanakhoza kukhala ali. Iye akanali moyo panobe usikuuno, chifukwa Khristu anachita izo. Nthawi yoyamba imene ine ndamuwonapo iye mu zaka zambiri. Ndikuyang'ana pozungulira pa omvetsera, kuziwona izo.

119 Mulungu akanali wamoyo. Ndiko kulondola. Ndipo Iye anati, "Chifukwa Ine ndiri moyo, inu mukhoza kukhala moyo nanunso."

120 Tsopano ine ndikanafuna kuti, kungoti ndikhale ngati ndiyike kwa inu chimene ichi chiri, chifukwa, ngati ine sinditero, ndiye inu mukhoza kuchokapo ndi kukati, "Chabwino, ine sindikuzimvetsa izo."

121 Tsopano, makani anga ndi awa, kuti, "Yesu Khristu akanali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Tsopano, ngati Iye akanali yemweyo, Iye ayenera kukhala yemweyo mu mfundo iliyonse, yemweyo mu—mu mphamvu, yemweyo mu nyonga, yemweyo mu chirichonse chimene Iye anali.

122 Ndipo akanali pansi pano, uko kunali Agriki ena, nthawi yina, omwe anadza ndipo anati, "Mabwana, ife tikanafuna kumuwona Yesu."

123 Ndipo ine ndikukhulupirira kuti icho ndi chokhumba cha munthu aliyense kapena mkazi yemwe anayamba wamvapo za Yesu, amafuna kuti amuwone Iye. Ndipo ngati Iye asali yemweyo, ndiye ife sitingakhoze kumuwona Iye. Koma ngati Iye ali yemweyo, ife tikhoza kumuwona Iye, kapena Iye anatiuza chinachake cholakwika. "Komabe kanthawi pang'ono, ndipo dziko silindiwona Ine kenanso, komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine," puronauni yaumwini, "Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mkati mwa inu mpaka ku mathero a m'badwo." Ndiyeno Yesu analonjeza kuti azikhala mu Mpingo Wake, kumachita zinthu zomwezo zimene Iye anali kuzichita apo, mpaka m'badwo uthe. Tsopano Iye anati, "Kanthawi pang'ono," dziko silimamuwona Iye kenanso. Chabwino, ndiye, ife tikanati tizimuwona chotani Iye? Ife tikanamachita kumauwona Mzimu Wake, ngati Iye ali mkati mwa ife, ndipo Mzimu umenewo ukanamati uzichita mofanana momwe Iye ankachitira apo, kapena Iwo sukanati ukhale Mzimu womwewo.

124 "Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi." Ndipo ngati ife tikubala . . . Ngati nthambi ili mu Mpesa, nthambi izibala mtundu wa chipatso chimene Mpesa umapereka kwa iwo. Chabwino, Mpesa woyamba umene ukutulukira apo . . . Nthambi yoyamba inachokera mu Mpesa inali nthambi ya chipentekoste; masomphenya, zimphamvu, machiritso, ubatizo wa Mzimu Woyera, zizindikiro zazikulu, ndi zodabwitsa. Nthambi yotsatira

ikanayenera kuti ikhale ya mtundu wofanana wa nthambi. Kupitirira mmusi mpaka ku mapeto, iyo iziyenera kuti ikhale yofanana. Ndicho chimene Yesu ananena.

125 Tsopano, tiyeni tiwone chimene Iye anali dzulo. Ngati ife tingakhoze kupeza chimene Iye anali dzulo . . . Tsopano ine ndikutenga mwa chidule, chifukwa cha nthawi; ndati ndipereke pafupi maminiti asanu a malangizo. Ndipo ngati ife tingakhoze kuwona chimene Iye anali dzulo, ndiye ife tingakhoze kuwona chimene Iye ali lero, ndipo akhala ali kwanthawizonse. Kodi izo ndi zosakondera mokwanira? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

126 Tsopano, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anabwera ngati Mesiya, anabatizidwa ndi Yohane M'batizi; anali asanachite ntchito ina apabe. Ndipo Iye analowa utumiki Wake woyambirira. Kodi Iye anatumizidwa kwa ndani? Ayuda.

127 Tsopano, ife tikuzindikira kuti pali mafuko atatu okha a anthu mu dziko, ndiwo: Ayuda, Amitundu, ndi Asamaria; amene ali anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti. Ayuda, Amitundu, ndi Asamaria.

128 Inu mukukumbukira? Petro anaitanira pa iwo, ndi mafungulo aku Ufumu, pa Tsiku la Pentekoste, kwa Ayuda. "Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mukhale obatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu."

129 Filipo anapita uko ndipo anakalalikira kwa Asamaria. Iwo onse anakhulupirira ndipo analapa, ndipo anali atabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Kungoti, Mzimu Woyera unali usanafike pa iwo. Petro anali ndi mafungulo. Iye anabwera uko ndipo anasanjika manja pa iwo, ndipo iwo analandira Mzimu Woyera.

130 Ndiyeno Kornelio, Wamitundu, anali ndi masomphenya, kuti iye anali woti atumize ndi kukamutenga munthu wotchedwa Petro, Simoni Petro, yemwe anali kukhala mu nyumba ya munthu yemwe anali wofufuta zikopa. Ndipo pamene Petro anabwera mpaka uko, "Petro akanali chiyankhulire Mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo." Ndiye Petro anati, "Kodi munthu angaletse madzi? Awa alandira Mzimu Woyera monga ife tinaupezera Iwo pa chiyambi." Nthambi iliyonse ikubwera apo mofanana basi. Mukuona?

131 Tsopano, pamene Yesu anakomana . . . Tsopano, Iye sanabwere kwa Amitundu. Ndi angati akudziwa izo? Iye anawaletsa ophunzira Ake kuti apite kwa Amitundu alionse. Ndi angati akudziwa izo? "Musati mupite mu njira ya Amitundu, koma mupite maka kwa nkhosa zosochera za Israeli. Ndipo pamene inu mukupita, kalalikireni, kumati, 'Ufumu wa Kumwamba uli pafupi,' kwa nkhosa zosochera za Israeli."

132 Tsopano, ndani anali kumuyembekezera kuti Iye abwere mu tsiku limenelo? Osati Amitundu; ife tinali achikunja,

Angelezi Achisaxon. Ife tinali Achiroma, tikupembedza dzuwa ndi zina zotero. Ife sitinali tikuyembekezera Mesiya aliyense, koma Ayuda ndi Asamaria anali. Tsopano, kodi Iye anadzilengeza chotani Iyeyekha kwa anthu amenewo omwe anali akumuyembekezera Iye?

133 Tiyeni tibwerere mmbuyo tsopano ku Yohane Woyera, mutu woyamba, ndipo kwa mphindi yokha tsopano. Ndipo mvetserani mwatcheru.

134 Myuda woyamba yemwe anayamba wabweretsedwa kwa Iye, pamene Filipo kapena . . . Andrea atatembenuzidwa, ndipo anapita nakamupeza m'bale wake, Simoni Petro, iye anamubweretsa Simoni pamaso pa Yesu. Ndipo Yesu anamuuza iye chomwe dzina lake linali, ndi yemwe abambo ake anali. Ndi angati akudziwa izo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Inu mukuganiza kuti icho chinachita chiani kwa munthu ameneyo, yemwe akanati kenako adzakhale ndi mafungulo aku Ufumu mu dzanja lake? Ndicho chimene Iye anadzitsimikizira Yekha kuti ali, Mesiya. Mwamsanga ndiye . . .

135 Filipo atatembenuzidwa, ndipo anapita kuti akampeze Nataniele. Ndiwo mailosi makumi atatu kuzungulira phiri. Ndipo iye anabwera mpaka ku nyumba, ndipo ine ndikukhoza kumumva iye akuti, "O, Akazi a Nataniele, kodi Nataniele ali kuti?"

"O, iye ali uko—mu munda wa azitona."

136 Anathamangira kunja uko mwamsanga kwenikweni, "Nataniele, kodi iwe uli kuti?" Ndipo iye anamupeza iye pansi pa mtengo. Ndipo Nataniele anali akupemphera. Ndipo iye anayembekezera mpaka iye atatsiriza kupemphera. Ndipo iye anati, osati, "Iwe uli bwanji, Nataniele? Mbewu zikuchita bwanji?" O, iye anali ndi uthenga! Ndi momwe munthu yemwe wakomana naye Yesu aliri. Iye alibe nthawi ya zopusa. Iye anati, "Tabwera, udzamuwone Yemwe ife tamupeza, Yesu waku Nazareti, mwana wa Yosefe!"

137 Ndipo tsopano ine ndikukhoza kumuwona Nataniele akusasa zovala zake, akuchokera pa pemphero. Iye anati, "Tsopano, Filipo, ine ndakudziwa iwe kuti ndiwe munthu wabwino, ndi munthu woonamtima. Tsopano, kodi kungakhoze kukhala chinthu chabwino chirichonse chingabwere kuchokera ku Nazareti? Chabwino, iwe ukudziwa, ngati Mesiya akanati abwere, Iye akanabwera ku Yerusalemu, kupyolera mu mpingo." Ndi chimene anthu akuganiza lero. Mwaona? "Iye akanabwera kupyolera ku Yerusalemu. A Kayafa sanalengeze konse izo pa msonkhano wathawu. Kotero, palibe mmodzi wa azamulungu wazilengeza izo. Chotero ine ndakudziwa iwe kuti ndiwe munthu woonamtima. Kodi iwe wapita ku mathero akuya?"

"O, ayi. Iwe ubwere udzapeze chomwe chiri."

Iye anati, "Kodi chirichonse chabwino chingakhoze . . . "

138 Iye anamupatsa iye yankho lopambana limene munthu aliyense akanakhoza, anati, “Bwera, udzadziwonere wekha.”

139 Tsopano, pa ulendo mozungulira, ine ndikukhoza kumumva Nataniele akuti . . . kapena Filipo akunena kwa Nataniele, “Iwe ukudziwa chiyani? Iwe ukumukumbukira nsodzi wachikulire uja uko yemwe sankakhoza ngakhale kulemba chiphaso chija pamene iwe unamupatsa iye zija, utagula nsomba zija kwa iye?”

“Inde. Ine ndikukhulupirira dzina lake linali Simoni.”

“Inde, ndi limenelo.”

140 “Ine ndinamubweretsa iye, tsiku lina, pamaso pa Mesiya ameneyo, ndipo mwamsanga pamene Iye anamuwona iye, Iye anati, ‘Dzina lako ndiwe Simoni. Dzina la abambo ako ndi a Yonasi.’ Ndipo ine . . . Sizikanati zikandidabwitse ine, kuti pamene iwe uti ukafike pamaso pa Iye, Iye nkusakuuza iwe yemwe iwe uli.”

Iye anati, “Aa, tsopano, dikirani miniti, osati ine.”

141 Chotero, tsiku lotsatira iwo anafika. Ndipo Yesu anali mu mzere wa pemphero, mwachizolowezi, akupempherera odwala. Ndipo pamene iye akanakhoza . . . anabwera apo ndipo analowa mkati mwa omvetsera. Yesu anayang’ana mmwamba, ndipo Iye anamuwona Filipo akubwera, akumubweretsa munthu kupyolera mu mpita. Ndipo Iye anayang’ana pa iye, ndipo Iye anati, “Taonani M’israeli mwa yemwe mulibe chinyengo.”

142 Chimenecho Chiphunzitso chachilendo? Ameneyo anali Yesu, dzulo. Uyo ndi Yesu, lero, ngati Iye ali yemweyo.

143 Ndipo munthu uyo anaima. Ine ndikukhoza kumuwona Nataniele. Filipo akumugunyuza iye, ndipo anati, “Ine ndinakuuza chiyani iwe? Ine ndinakuuza chiyani iwe?”

144 Iye anati, “Rabbi,” zikutanthauza *mphunzitsi*, kapena chirichonse chimene ife timachitcha icho lero, inu mukudziwa. Kwenikweni, mawu olondola Achihebri, amatanthauza *mphunzitsi*. Anati, “Rabbi, ndi liti lomwe Inu munayamba mwandiwonapo ine? Inu mwadziwa motani chirichonse za ine? Ine sindinayambe ndakuwonani Inu mu moyo wanga. Inu mwadziwa motani kuti ine ndine M’israeli? Inu mwadziwa motani kuti ine ndine wolungama, ndi woonamtima, ndi wonena zoona? Inu simunayambe mwandiwonapo ine, mu moyo Wanu. Inu mwandidziwa motani ine?”

145 Iye anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo, Ine ndinakuona iwe,” mailosi makumi atatu kuzungulira phiri, dzana lake. Ndi maso otani!

146 Tsopano kodi iye ananena chiyani? Iye anati, “Rabbi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu. Inu ndinu Mfumu ya Israeli.” Ngati Ayuda anachizindikira icho . . . Tsopano dikirani. Uyo anali Myuda wosankhidwa. Ndi angati amakhulupirira mu kusankhidwa? O, alipo anthu ambiri amene sadzalandira konse

izo. Mukuona? Baibulo linanena chomwecho. Koma munthu ameneyo anali ndi Mzimu wa Mulungu mwa iye. Ndipo iye anavomereza izo, anati, "Rabbi, Ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli."

147 Koma kumeneko kunaima wazamulungu wa tsiku limenelo, ansembe ndi aphunzitsi aakulu, akumvetsera kwa Iye. Ndipo inu mukudziwa chimene iwo ananena? Iwo anati, "Iye ndi wam'bwebwe. Iye ali ndi mzimu wa Belezebule pa Iye." Yesu . . . Iwo sanali kuyankhula izo, mokweza. Ayi, ayi.

148 Koma Yesu anapotoloka ndipo anayang'ana pa iwo. Iye anati, "Inu mukhoza kunditcha Ine izo ndi kudutsa nazo izo. Koma ili kubwera nthawi pamene Mzimu Woyera uti udzabwere, ndipo pamene inu muyankhula mawu amodzi momutsutsa Iye akuchita chinthu chomwechi, izo sizidzakhululukidwa konse mu dziko lino kapena dziko liri nkudza."

149 Chotero ndiye kodi ife tikuchita ndi chiyani? Awo anali Ayuda. Ayuda enieni ndi owonamtima anamukhulupirira Iye kuti anali Mesiya.

150 Aphunzitsi ndi azamulungu, kodi iwo anali ndani? Mbewu ya serpenti, monga ife tadutsiramo. Iye anati, "Inu ndinu a atate wanu, Mdierekezi." Komabe, iwo anali ophunzira, anzeru, amuna oyera. Iwo sankakhoza kusuntha kaphesi . . . Oyera. Iwo sankakhoza kuswa Sabata. Iwo sankakhoza kudya nyama. Iwo anali amuna oyera, koma iwo analephera kuti awone. Mukuona, iwo anali ataphunzitsidwa ndi anthu.

Mulungu amaphunzitsa amuna Ake, molimba. Ndiko kulondola. Amuna oitanidwa ndi Mulungu!

151 Ndiye tsiku lina Iye—Akanati . . . Ndizo zomwe Ayuda ankaganiza. Ndi momwe Iye anadzipangitsa kudziwika Iyeyekha kwa Ayuda. Ndi angati akudziwa kuti ndilo Lemba? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Chabwino. Tsopano, ngati Iye anadzipangitsa kudziwika Iyeyekha kwa Ayuda, ameneyo anali Yesu dzulo ndi Ayuda.

152 Tsopano inu mukuti, "Asamaria anali akuyembekezera kuti Iye abwere." Inde, iwo anali, koma osati Amitundu. Asamaria okha.

153 Ndipo pamene Iye anakomana ndi Asamaria koyamba, Iye ankasowa kuti adzere ku Samaria. Ndipo Iye anaima, ndipo anawatuma ophunzira Ake, apite akafune chakudya, pafupi thwelofu koloko. Iye anakhala pansi pa chitsime. Apo panatulukira mkazi, anayamba . . . Tsopano, ife tikudziwa iye, mu dziko ili, kuti anali mkazi wa mbiri yoipa, dona wa mumsewu, inu mukudziwa, wachiwerewere. Ndipo chotero iye anatulukira ndipo anayamba kutsitsira chidebe pansi mu chitsime, kuti atungepo madzi. Ndipo iye anamva Liwu likuti, "Mkazi, ndibweretsere Ine akumwa." Ndipo iye anayang'ana pozungulira ndipo apo panakhala Myuda wa usinkhu wapakati.

154 Iye anali wa makumi atatu okha ndi chinachake, koma Baibulo linati Iye ankawoneka wa makumi asanu. Iwo anati, "Ndiwe Mwamuna wosapitirira usinkhu wa zaka makumi asanu, ndipo ukuti Iwe 'unamuwona Abrahamu'?"

155 Iye anati, "Asanakhalepo Abrahamu, Ine ndine." Mukuona? Ayenera kuti ankawoneka wachikulire chifukwa cha ntchito Yake, thupi Lake laumunthu.

156 Ndipo iye anayang'ana apo. Iye anadziwa kuti Iye anali Myuda. Iye anati, "Bwana, si mwambo wake kuti inu Myuda muwapemphe Asamaria zinthu zoterozo monga izo. Ife tiribe chochitirana chirichonse wina ndi mzake."

157 Iye anati, "Mkazi, ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe unali kuyankhula naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa. Ndipo Ine ndikanakubweretsera iwe, ndikanakupatsa iwe madzi amene sukanati uzibwera kuno kuti udzatunge." Kodi Iye anali akuchita chiyani? Kuwukhudza mzimu wake. Mukuona? Penyani, Iye akuti adzilengeze Iyeyekha kwa Asamaria, tsopano.

158 Ndipo iye anati, "Bwanji, Inu mumati, 'Kumakapembedza ku Yerusalemu.' Ife timati, 'Mu phiri ili.'"

159 Iye anati, "Nthawi ili nkudza, ndipo tsopano ili, pamene inu simudzatero, mu phiri ili kapena ku Yerusalemu, kumupembedza Mulungu, koma mu Mzimu ndi Choonadi. Atate akufuna oterowo."

160 Kodi Iye anali akuchita chiyani? Kuwugwira mzimu wake. Ndipo patapita kanthawi, pamene Iye anapeza pamene vuto lake linali . . . Ndi angati akudziwa chimene vuto lake linali? Iye anali ndi amuna asanu, ndipo iye anali akukhala ndi wachisanu ndi chimodzi. Kotero, Iye anati, "Mkazi, pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno."

Iye anati, "Ine ndiribe mwamuna aliyense."

161 Anati, "Ndiko kulondola. Iwe uli . . . unali nawo asanu, ndipo mmodzi yemwe iwe tsopano ukukhala naye si wako."

162 Iye anaima ndipo anayang'ana pa Iye. Tsopano, iye sanati, "Ndinu Belezebule, bwana. Inu ndi wam'bwebwe." Iye ankadziwa mochuluka za Mulungu kuposa theka la alaliki aku Jeffersonville, ndiko kulondola, pokhala wachiwerewere. Iye anati, "Bwana, ine ndadziwa kuti Inu ndinu mneneri."

163 Penyani, "mneneri." Ndipo ngati inu mungawayendetse mawu amenewo chammbuyo, inu muwapeza iwo, Mneneri yemwe Mose anati akanati adzabwere, mukuona, "Ambuye, Mulungu wanu, adzadzutsa mneneri wonga ine."

164 Iye anati, "Ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri." Iye anadziwa kuti Iye sanali kuzidziwa izo mulimonse; sakanakhoza kuzidziwa izo. Anati, "Ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri." Tsopano mvetserani pano, "Ife, Asamaria," osati Ayuda tsopano. Asamaria, "Ife tikudziwa, pamene Mesiya abwera, Iye adzatiuza

ife zinthu izi." Mukuona mtundu wa chizindikiro iwo anali kuchiyembekezera? Chizindikiro cha Mesiya. "Pamene Mesiya abwera, Iye adzatiuza ife zinthu izi, koma Inu ndinu yani?"

Iye anati, "Ine ndine Iye, yemwe akuyankhula ndi iwe."

165 Ndipo iye anagwetsa chidebe chake chamadzi, ndipo anathamangira ku mzinda, ndipo anati, "Bwerani, mudzamuwone Mwamuna yemwe wandiuza ine zinthu zomwe ine ndachita. Kodi ameneyu si Mesiya?"

166 Ngati icho chinali chizindikiro cha Mesiya pamenepo, icho chiyenera kukhala chizindikiro cha Mesiya lero. Ngati Iye ali . . . Tsopano, kumbukirani, palibe nthawi imodzi pamene chozizwitsa icho chinayamba chachitidwapo pamaso pa Amitundu. Izo zinali zoletsedwa. Chifukwa? Amitundu anali ndi zaka zikwi ziwiri za mwachimpingo.

167 Koma tsopano kutha kwa m'badwo wa Amitundu kuli pano. Ndipo Russia, chikominisi, chalozetsa bomba kumene cha kwa inu, kuti alithetse ilo, naponso. Musati muzidandaula, izo zikubwera. Baibulo linanena chomwecho. Ilo lidzakhala kuno ndi dzina lanu litalembedwa pa ilo, ndipo ilo lidzasandulika phulusa mu nthawi ya mphindi imodzi, fuko lonse. Ilo lidzakhala litathetsedwa kwathunthu. Zindikirani, uyo ndi Mulungu akuchita izo. Ine ndikudziwa kuti iwo ali ufumu waufulu, iwo ndi gulu la achikunja. Koma kodi Mulungu sanadzutse mafuko achikunja kuti amuwongole Israeli mu masiku apitawo? Baibulo limanena kuti Russia ndi chikominisi zikusewera kumene mmanja a Mulungu, kuti athetse anthu mwamtheradi pa dziko lapansi.

168 Koma izo zisanati zichitike, Mkwatulo ukubwera ndi kudzautengera Mpingo Kwawo izo zisanafike pochitika. Ndipo ngati izo zayandikira pafupi chotero, Mkwatulo uli pafupi chotani? Pafupiko kuposa izo. Chotero inu mukuona chifukwa ife tiri . . . chifukwa ine ndikulalikira momwe ine ndikuchitiramu, pamene ine ndikulimbikira molimba monga ine ndingathere; pamene Mulungu akuchita chirichonse chimene Iye angakhoze kuchita, kuti akanikizire izo mwa Osankhidwa, kuti akokere Mbewu ya mkazi kunja, kuti mbewu ya serpenti ikhoze kutenga chilango. Ndiko kulondola ndendende. Ndizo zimene Iye analonjeza kuti adzachita.

169 Tsopano, ngati Yesu anadzilengeza Iyeyekha pamaso pa Myuda ndi pamaso pa Msamaria, mwa zizindikiro zimenezo, ndipo akatilola ife kuti tizipita wopanda kulengeza chizindikiro chomwecho kwa ife, Iye ali wosalungama; ngati Iye atisiya ife kuti tidutse nazo, mwa kuti, "Ndife Amethodisti. Ndife Abaptisti. Ndife Akatolika. Ndife Apresbateria." Ayi, bwana, Iye akatilola ife kuti tidutse nazo ndi zamulungu zozizira.

170 Iye ayenera kuti abwere ndi zizindikiro, zodabwitsa, basi monga Iye anachitira mu malo oyamba, ngati Iye ali yemweyo

dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ife tafika pa tsiku limenelo. Ife tiri pano tsopano. Mwa Baibulo, mwa mboni, mwa Mzimu, mwa sayansi, chirichonse chikutsimikizira kuti liri pano. O, ine . . . O, ine ndikukhumba ine ndikanakhala ndi mphamvu kuti ndikankhire izo mwa anthu, kuti ndiwalole iwo kuziwona izo.

171 Inu anthu kuno mu Jeffersonville ndinu anthu anga. Ine ndaleledwa ndi inu. Ndipo ine—ine ndimakukondani inu. Musati—musati mundiganizire ine kuti ndine wotentheka. Kodi inu mukuganiza zoneneratu izi ziri? Tayang'anani mmbuyo ku kusefukira kwa '37, inu anthu, pamene inu munkaseka pomwe pano pa mpingo. Ndipo ine ndinati, "Iwo adzakhala mapazi makumi awiri ndi awiri pa Spring Street," miyezi isanu ndi umodzi izo zisanachitike. Ndiuzeni ine nthawi imodzi pamene chirichonse chinayamba chanenedwapo, cha PAKUTI ATERO AMBUYE, chimene sichinali ndendende Choonadi. Ndiuzeni ine chinthu chimodzi chimene chinayamba chanenedwa. Palibe! Ndi Choonadi, ndipo Icho chatsala chikadali Choonadi, ndipo Icho nthawizonse chidzakhala chiri Choonadi.

172 Tsopano ife sitingakhoze kubweretsa . . . Ine ndikulingalira alipo zana kapena anthu opitirira pano oti apemphereredwe. Ife sitingakhoze kuwabweretsa iwo onse mwa kamodzi. Ife tiwabweretsa omwe ife tingakhoze, pa nthawi, ndiyeno tiziwabweretsabe iwo mpaka ife titawabweretsa iwo onse pano. Tsopano ine ndikuti ndiyambire mu . . . Ine ndikukhulupirira. Kodi Billy Paul sanali pano? Kodi iye ali kumbuyo uko? Muuzeni iye kuti abwere kuno. Ine ndikufuna ndiwone chiyani, ngati iye anapereka . . . Iwe unapereka khadi yanji? [M'bale Billy Paul ati, "Q, wani mpaka handiredi."Mkonzi.] Ma Q, Q, Q. Khadi la pemphero Q. Yang'anani pa khadi la pemphero lanu. Ilo liri ndi Q. Wani mpaka handiredi. Chabwino. Ife sitingakhoze kuwabweretsa iwo onse pa nthawi imodzi, koma ife tikhoza kungobweretsa pang'ono pokha pa nthawi, mpaka ife titakhoza kuwabweretsa iwo onse pamwamba pano. Ife tikufuna kuti iwo kuti azibwera, mmodzi ndi mmodzi, mpaka iwo onse atapemphereredwa.

173 Tsopano penyani. Ine ndikufuna aliyense, mkati ndi kunja, kuti aganize za izi. Ndipo potseka pa msonkhano uno, ine ndikuwupereka mpingo uno kwa m'busa, M'bale Neville, kukuperekani inu kwa iye, ndi iye kwa Mulungu. M'bale Neville pano. Ine ndikukuitanani nonse inu kuti mubwerenso. M'bale Neville ndi msirikali wamphamvu. Iye ndi wantchito weniweni wa Khristu. Mlaliki wa Chimethodisti poyambapo, ine ndikukhulupirira, wophunzira wochokera ku Asbury, ndipo iye anali ataphunzitsidwa mu zamulungu zonse, seminale ya zamulungu, ndi kujayira kwa zomwe iwo amaphunzitsa. Koma, tsiku limodzi, iye anafika pa malo pamene iye anadziwa kuti iye ankayenera kuti akhale ndi chinachake chosiyana, ndipo iye anawoloka mzere. Iye ndi m'busa pano, mwamuna wodzazidwa

ndi Mzimu, mlaliki weniweni, wazamulungu weniweni. Ndipo ine ndikukupemphani inu, anthu a mzinda uno, ndi mu chigawo chino, ngati inu mulibe mpingo, ndipo inu mukufuna kuti muzimvera Uthenga weniweni, muzibwera kudzamumvera M'bale Neville. Iye amaimira Chinthu chomwecho chimene ine ndimachita. Mwamtheradi, msirikali weniweni wamphamvu. Ife tonse, pano, timamukonda M'bale Neville. Iye wakhala ali pano ndi ife nthawi yaitali, ndipo ife timamukonda iye.

174 Tsopano ngati Yesu Khristu, mwa Mzimu, ati abwerere kuno usikuuno ndi kudzachita zinthu zomwezo zimene Iye anachita pamene Iye anali pano pa dziko lapansi, kwa Myuda ndi Msamaria, Iye achita chinthu chomwecho kwa inu Amitundu, ndi angati a inu muti munene, "Ine ndimukhulupirira Iye ndi mtima wanga wonse ndipo ndikuzilandira izo pomwe pano"? Sindikusamala mpingo womwe inu muli a iwo. Izo ziribe . . .

175 Inu mukuti, "Kodi inu mukufuna kuti ine ndisiye kumapita ku mpingo wa Methodisti?" Ayi, bwana. "Baptisti?" Ayi, bwana.

176 Inu muzipita kulikonse kumene inu mukukufuna kumatero, pakuti Mulungu ali nawo ana mu umodzi uliwonse wa mipingo imeneyo. Ndithudi, Iye ali nawo. Ndipo inu, mwinamwake, ndinu mmodzi wa iwo. Ndipo ine ndikukukondani inu mofanana basi monga inu mukanakhala membala wa Branham Tabernacle. Izo sizimapanga kachidutswa kamodzi ka kusiyana kwa ine. Inu mukudziwa izo mwa utumiki wanga, kulikonse. Ine ndikukhulupirira Mulungu amawakonda ana Ake, ziribe kanthu mtundu wanji wa chizindikiro chomwe iwo akugwirapo. Ndi chimene inu muli mu mtima mwanu. Koma ife tikungokuitanirani inu ku chiyanjano. Ndinu olandiridwa kuti mubwere.

177 Tsopano, aliyense amadziwa, ndipo inu anthu aku Jeffersonville mukudziwa, pambuyo pa zinthu zambiri zonse zimene zanenedwa ndi kuchitidwa, ndi kunenedweratu, chimodzi chirichonse cha izo kufika pakuchitika mwangwiro basi . . . Ndi angati kuno mu Jeffersonville akudziwa kuti izo ndi choonadi? Kwezani mmwamba manja anu amene mukudziwa kuzungulira kuno tsopano. Tsopano, kwa inu anthu akunja kwa mzindawu, inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndi angati akunja kwa mzindawu amene anayamba akhalapo mu misonkhano yanga ndipo anawona kuti izo zimachitika chimodzimodzi basi monga Iwo amanenera? Kwezani manja anu, kwa anthu aku Jeffersonville. Mukuona? Baibulo linati, "Pa kamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu mulole mawu aliwonse akhale okhazikika." Kuzungulira mdziko izo zakhala ziri. Ndiye ife tikuyembekezera chiyani? Ife tiri nacho chirichonse mmanja athu momwe, ndi Ambuye Yesu. "Iye watipatsa ife zinthu zonse mwaulele."

178 Tsopano ife tiyamba mzere wa pemphero. Ndipo ngati Yesu Khristu ati achite pano usikuuno . . .

179 Tsopano, ndi angati a inu mukudziwa za chithunzi cha Ambuye Yesu, Kuwala kuja? Nonse a inu mukudziwa za Icho, mwakuchitika. Icho chiri mu Washington, D.C., chinajambulidwa ndi munthu wopambana yemwe Edgar Hoover anali naye mu zaka pang'ono zapitazi, George J. Lacy, mpukutu wa zidindo za zala. Ife tiri nako—kusaina kwake kuli pa pepala kumene. Icho, makamaka . . . Iye anati iye pena ankaganiza kuti kunali kuwerenga maganizo, ine ndinali kuwerenga maganizo a anthu. Iye anati, "Koma, Bambo Branham, diso la makina la kamela iyo silingakhoze kutenga kuwerenga maganizo." Anati, "Kuwala kunakhudza disolo." Ndipo ife tiri nazo izo zitalembedwa pa pepala, zikupita kunja limodzi ndi chithunzi, Kuwala kunakhudza disolo.

180 Ndi angati akanali moyo, pamene Iko kunayamba kuwonekera pamaso pa anthu kumusi kuno pa mtsinje, pamene ine ndinali kuwabatiza iwo mazana kumusi kuja tsiku lija? Mu nyumbayi, kwezani mmwamba dzanja lanu. Apo pali manja atatu kapena anai, akadali moyo, ochokera ku zaka zapitazo, kumusi kuno pa mtsinje pamene Iko kunabwera pansi, ndipo Uthenga wa Ambuye unabwera. Mofanana kumene basi! Kodi Iko kunachita chimene Iko kunanena uko? Kuti, utumiki umene ine ndikanati ndikhale ndikulalikira, ukanati udzayambitse chitsitsimutso chozungulira mdziko, kutangotsala pang'ono Kudza kwachiwiri kwa Khristu. Penyani chimene Iko kwachita. Mwaona? Mmenemo munatuluka, kuchokera umo, Oral Roberts ndi ena onse awa. Mwaona? Ndipo kuzungulira dziko izo zapita, fuko lirilonse, anthu aliwonse, chinenero chirichonse. Moto wa chitsitsimutso ukuyaka, misonkhano yayikulu ya machiritso. Mwaona?

181 Tsopano, khalani okonzeka. Mkati, kunja, kulikonse inu muli, mulandireni Khristu. Mutero inu, usikuuno?

182 Tsopano, kuchokera pano mpakana, ine ndikudzipereka ndekha kwa Ambuye Yesu, kuti ine ndikakhoze kukwanitsa kudzipereka ndekha kwa Mzimu, kuti ndizingomkuza Yesu Khristu yekha; osati inemwini, koma Yesu Khristu; kuti anthu awa, anthu anga, abwenzi anga, mkati ndi kunja kwa mzinda, akakhoze kudziwa kuti Uthenga umene ine ndaulalikira uli . . . mwamtheradi Choonadi. Ndipo Khristu ali pano kuti awutsimikizire Iwo kuti uli Choonadi, mwa Mawu Ake ndi Mzimu Wake.

183 Ife tichita kumawaitana iwo mmodzi pa nthawi. Chotero ife tikhala . . . Ife tiyambira ndi nambala wani, Q nambala wani. Ndi ndani ali nayo iyo? Ngati—ngati inu simungakhoze kuwuka tsopano, akulu adzakunyamulani inu. Ife tikufuna kuti timutenge mmodzi aliyense wa inu. Q nambala wani.

M'bale Hickerson, Billy Paul . . . Kapena, dikirani, Doc akuti amuthandizire iye pano. Q nambala wani, kodi inu mungakwezere mmwamba dzanja lanu, yense yemwe ali nayo iyo. Kodi inu mukutsimikiza kuti iyo inali Q? Kapena, chabwino, o, ine ndikupepesa. Chabwino. Bwerani komwe kuno. Msonyezeni iye kachitidwe kache, kudzera mu kampita uko. Q nambala wani. Chabwino.

184 Nambala thuu, kwezani dzanja lanu, chonde. Chabwino, dona wakhala kumbuyo komwe mkati *muno*. Chabwino, dona, bwerani. Pangani njira mpaka cha *kuno;* ngati inu nonse mungati mumulole iye. Anyamata uko akuthandizani inu, othandizira ndi ena otero. Q nambala firii, kwezani mmwamba dzanja lanu. Nambala firii. Kodi mungakweze dzanja lanu, yense yemwe ali ndi Q nambala firii. Onani ngati dona uyu yemwe akupita apayu, ngati iye ali nalo khadi. Inu—inu mulibe iyo? [Mlongo ati, "M'bale Branham, ine ndinapempha khadi. Koma ine ndinamuwona mzanga wa ine, yemwe anaima ndi mnyamata wodwala."—Mkonzi.] Inu—inu simungakhoze kuchita izo. ["Simungakhoze?"] Ayi. Inu muyenera kuigwira iyo ndi kumvetsera kwa malangizo. Ife timutenga mwanayo, mulimonse. Mukuona? Inu muzingobwera pamene nambala yanu yaitanidwa. Mwanayo akhoza kubwera pamene iyo yaitanidwa. Mukuona? Ndi zabwino.

185 Nambala wani, thuu. Ndi ndani yemwe ali nayo nambala firii? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Nambala firii. Nambala folo.

186 Tsopano, ndizo zokondeka mwamphamvu kwa inu, mlongo, yense yemwe iye anali, dona uja yemwe amafuna kuti achite izo. Mukuona? Koma, onani, ngati—ngati nambala yawo yaitanidwa, iwo azibwera basi . . . Ngati iwo sanaitanidwe, ife tiwatenga iwo, mulimonse. Mukuona? Ife tikukufunani inu mu malo anu basi, kotero inu mukhoza kukhala ndi malo anu, inunso, inu mukuona. Mukuona? Chabwino.

187 Nambala firii. Nambala folo. Nambala faifi. Q nambala faifi, kwezani mmwamba lanu . . . Kumbuyo komwe, mkazi wamng'ono. Nambala sikisi. Chabwino, mnyamata wamng'ono. Nambala seveni. Mwamuna komwe kuno. Nambala eyiti.

188 Ife tiyenera kuti tichite izi. Inu mukuona, inu simungakhoze kuchita izo; mumangofika pongodzazana monse, inu mukati, "Munthu aliyense akufuna kuti apemphereredwe."

189 Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu chinachake, ngati inu mukufuna kuti muwone chifukwa chimene ife timachita kuwafolela iwo. Aliyense mkati muno yemwe akanafuna kuti abwere ndi kuti adzapemphereredwe, kwezani mmwamba manja anu, munthu aliyense, ziribe kanthu yemwe inu muli. Taonani apo. Ndani yemwe ati abwere choyamba? Mukuona? Payenera kukhala winawake.

190 Billy amabwera kuno, amawatenga makadi awa, ndipo amawasakaniza iwo onse pamaso pa inu, ndipo iye amamupatsa aliyense khadi la pemphero yemwe akufuna imodzi. Inu mukhoza kutenga yachisanu, yachisanu ndi chimodzi, ndipo nthawizina ife timayambira penapake. Ndipo izo sizimapanga kusiyana kulikonse pamene ife . . . Ndiyeno iwo kunjako mwa omvera amachizidwa kwenikweni asanatero awa a pa nsanja, nthawizina. Ndi angati akudziwa izo, onse alendo ndi . . . Chabwino, zedi, ziribe kanthu kochita ndi izo.

191 Nambala sikisi, mmodzi ameneyo wabwera? Nambala seveni. Nambala eyiti. Ndi ndani yemwe ali ndi khadi la pemphero eyiti? Takhala nayo kale iyo? Nambala naini.

192 Eyiti, nambala eyiti, ife tikufuna inu kuti muitenge iyo tsopano. Mwina winawake kunjako. Ngati iwo ali, winawake akweze dzanja lawo, kapena chinachake, winawake kunjako, yemwe sakanakhoza kuti alowe mkati. Nambala eyiti. M'bale Collins, kodi alipo aliyense kumbuyo uko, khadi la pemphero nambala eyiti, yemwe akuyesera kuti alowe mkati? Chabwino, khadi la pemphero nambala eyiti. Chabwino.

193 Nambala naini. Khadi la pemphero naini, kwezani mmwamba dzanja lanu. Mwina iwo anapita panja, sakanakhoza kulowa mkatimu. Ngati iwo ati abwere muno, ayikeni iwo mu mzere.

194 Nambala teni, kwezani mmwamba dzanja lanu. Mwamuna kutali uko mmbuyo. Bwerani, bwana. Wokondwa kukuwonani inu mukuitanidwira mkati. Inu munali mutaima kumbuyo uko, miyendo itachita zanzi. Nambala teni.

195 Nambala leveni. Kwezani mmwamba dzanja lanu, yense yemwe ali ndi khadi la pemphero Q nambala leveni. Chabwino, leveni.

Thwelofu, Q nambala thwelofu. Njira . . . Chabwino, thwelofu.

196 Satini. Satini. Ingokwezani mmwamba dzanja lanu, chonde, kuti ine ndikhoze kuliwona. Khadi la pemphero satini, Q satini. Fortini. Fortini. Fifitini. Kodi unapereka makadi angati, Billy, zana? Satini, fortini, ndi fifitini, akusowa. Khadi la pemphero satini, fortini, ndi fifitini, kodi inu muli pano? Fifitini, sikisitini, seventini, eyitini, naintini, twente.

197 Q poyamba, ndiye kuti titenge J, ndiyeno nkumangopitirira mmusi pa mzere. Ine ndikuganiza iwo akuyesera kuti atsirize awa, poyamba, mwaona. Ife tikatha kuwaitana iwo, ife tifika kwa enawo basi pamene titi tizibwera. Mukuti chiyani? [M'bale akuyankhula—Mkonzi.] Ndi choncho. Inu mukuona, ife tinapereka makadi uko, mmawa uno, ndipo anthu sanabwerere, mwinamwake. Mukuona? Chabwino.

198 Tiyeni tiyambire pamenepo pang'ono. Motani . . . Inu muli pafupi kukwanitsa mzere wanu uko tsopano? Chabwino. Tsopano, ndi ndani yemwe ali nayo fifitini, sikisitini, seventini, eyitini, naintini, ndi twente, mu ma Q? Twente wani, twente-thuu, twente-firii, twente-folo, twente-faifi. Tsopano ingokhalani muli ok onzeka, basi mwamsanga izi zikakhala zitatha. Ife tiri ndi mzere wodzaza pano tsopano. Ndiyeno ife tibwera mpaka kwa iwo, kupita mopitirira mpaka pansi pa mzere, ndiye nkulumphira mpaka mu makadi onsewo, ma J, pamene ife tinalekezerapo, ndi mmusi momwe mpaka ife tifike pa mapeto a iwo nkutha.

199 Tsopano ingokhalani molemekeza kwenikweni kwa mphindi pang'ono. Tsopano, ine ndikukhumba ife tikanakhala ndi malo okhalamo. Ine ndikukhumba pakanakhala pali njira ina yomwe ine ndikanati ndizichitira izo, koma ife tiribe iyo. Koma, tsopano, ine ndikufuna kuti inu mungokhala mwakulemekeza. Tsopano, kukanali molawirirabe. Ili maminiti khumi isanakwane naini. Msonkhano ukhala utatha, theka lina la ora. Chotero, uku ndi kutsekera kwa msonkhano, ndipo chotero tsopano khalani molemekeza kwenikweni. Khalani chete kwenikweni. Musati muziyendayenda.

200 Ndipo ndi angati mkati muno amene alibe khadi la pemphero, ndipo komabe inu mukufuna kuti mupemphereredwe? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino, iwo angokhala paliponse. Tsopano, ngati inu mulibe khadi la pemphero, ine ndikufuna kuti ndikupatseni inu Lemba lina.

201 Nthawi ina Ambuye wathu anali akupita kuti akamuwukitse msungwana wamng'ono, wakufa, yemwe anali asanafe apobe, mwana wamkazi wa Zakeyu. Ndipo mkazi anati mu mtima mwake, "Ine ndikumukhulupirira Iye kuti ndi Munthu woyera. Ine ndikumukhulupirira Iye kuti ndi Mesiya." Ndipo iye anali ndi vuto la magazi kwa zaka zambiri. Ndipo iye anazembera mu unyinji ndipo anakagwira chovala Chake. Munayamba mwawerengapo nkhaniyo?

Ndipo Yesu anaima, anati, "Ndani wandigwira Ine?"

202 Ndipo Petro anamudzudzula Iye. Iye anati, "Chabwino, onse a iwo akukugwirani Inu. Ndipo bwanji Inu mukuti, 'Ndani wandigwira Ine?'"

203 Iye anati, "Ine ndafooka. Ukoma, mphamvu, zachoka mwa Ine." Mukuona chimene izo zimachita kwa iwe, masomphenya? "Ine ndafooka. Mphamvu zachoka mwa Ine."

204 Ndipo Iye anayang'ana pozungulira, pa omvera, mpaka Iye anamupeza mkazi. Iye anachita mantha. Iye ankaganiza kuti iye anali atachita chinachake cholakwika. Koma Iye anayang'ana pa iye, ndipo Iye anamuuza iye za kutaya kwake kwa magazi, ndipo anati, "Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe."

Ndi angati akudziwa izo kuti ndi Choonadi? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

205 Tsopano, kwa inu masikolala a Baibulo, kodi Baibulo limati, kuti, "Yesu Khristu pakali pano ndi Wansembe Wamkulu, Wansembe wathu Wamkulu, yemwe angakhoze kugwiridwa ndi kumverera kwa zowawa zathu"? Ndi angati akudziwa izo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Chabwino, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu tsopano yemwe angakhoze kugwiridwa ndi kumverera kwa zowawa zathu, Iye akanakhoza kuchita motani, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Iye akanayenera kuti achite mwanjira yomweyo momwe Iye ankachitira pamenepo. Kodi uko ndi kulondola? ["Ameni."]

206 Chabwino, tsopano, Iye alibe thupi logwirika tsopano, pakuti ilo liri ku dzanja lamanja la Mulungu. Koma Iye ali nawo matupi athu amene Iye amagwiriramo ntchito, ndipo ndi Mzimu Wake ukugwira ntchito kupyolera mwa ife, monga Iye anati iwo unali. "Ine ndidzakhala ndi inu, mkati mwa inu; ntchito zimene Ine ndikuzichita, mudzachita inunso. Zochuluka kuposa izi inunso mudzazichita, zochuluka, pakuti Ine ndikupita kwa Atate." Iye akanati adzaime mu malo athu. Mwaona? Koma Iye akanati azitidzoza ife ndi Mzimu.

207 Tsopano, inu kunja uko mwa omvera, inu mungoyang'ana cha kuno. Ndipo musati muzingoyang'ana pa ine monga M'bale Branham. Inu muzingoti, "Ambuye Yesu, Ndinu Wansembe Wamkulu, ndipo Inu muli mu nyumba muno. Ndipo ine ndikufuna kuti ndikugwireni Inu ndi zowawa zanga, kukuuzani Inu, ine ndikudwala. Ndipo Inu mutsimikizire izo ndi ine, ndipo mungomulola M'bale Branham kuti atembenuke apo monga, ndi Mzimu Wanu, ndipo andiuze ine monga Inu munamuuzira mkazi uja. Izo zikhazikitsa icho." Ine ndikupikisana nacho chikhulupiriro chanu, mu Dzina la Ambuye, kuti muchite izo. Tsopano penyani ngati izo ziri zolondola kapena ayi. Inu mumufunse Mulungu izo, ndipo muwone ngati izo ziti zichitike basi mwanjira imeneyo. Tsopano ingokhalani molemekeza kwenikweni.

208 Tsopano inu mukhoza kubweretsa odwala anu. Kapena, kodi munthuyo anali uyu? Chabwino. Chinthu choyamba mu mzere, gawo ili la mzere . . .

209 Alipo anthu ochuluka muno. Ife timayesera kuwasiya anthu kutali, anthu aku Jeffersonville; kungowalola anthu a kunja kwa mzinda, kulimbanira kuti alowe muno. Chifukwa, mu mzere wa mtundu uwu, ngati anthuwo anali ochokera kuno, kuzungulira Jeffersonville, iwo akanakhoza kunena, "Bwanji, M'bale Branham amawadziwa anthu amenewo. Zedi, ndi chimene izo ziri." Koma, ndithudi, iwo sanayambe akhalapo mu Afrika, ndi India, ndi Asia, ndi Ulaya, ndi konse kuzungulira dziko, mu malo ena. Koma ine sindikudziwa izo.

210 Ine ndikukhulupirira, anthu onse awa mu mzere uwu apa tsopano, akuwoneka kwa ine ngati iwo ali alendo kwa ine. Kodi inu nonse ndinu alendo kwa ine? Ingokwezani mmwamba manja anu ngati inu muli. Chabwino. Ndizo zabwino. Ndi angati kunjako kwa omvetsera ali alendo kwa ine, kapena inu mukudziwa kuti ine sindikudziwa chomwe chavuta ndi inu? Basi munthu aliyense, ziribe kanthu yemwe iye ali. Zedi, inu simuli, mwaona. Koma Iye amatero. Tsopano, ine sindikunena kuti Iye atero. Koma ngati Iye ati atero, ndiye izo zimupangitsa Iye kukhalapo pomwe pano.

211 Tsopano, bambo uyu pano, ine ndikukhulupirira, anakweza dzanja lake, kuti iye ndi ine tinali alendo kwa wina ndi mzake. Ife ndife alendo. [M'bale ati, "Kulondola."—Mkonzi.] Ine sindinayambe ndamuwonapo bamboyu mu moyo wanga. Ine ndiri . . . ["Ine sindinayambe ndakuwonanipo inu."] Iye sanayambe wandiwonapo ine mu moyo wake mpaka tsopano pakali pano. Ife tabwera mnyumba muno, ndipo ife taonana wina ndi mzake tsopano kwa nthawi yathu yoyamba.

212 Tsopano, pano pali chithunzi changwiro cha Filipo kupita, kukamutenga Nataniele, ndipo Nataniele nkubwera pamaso pa Yesu. Tsopano, osati kuti iyeyo ndi Nataniele, kapena ineyo Yesu. Tsopano, musati muziganiza izo. Koma zaka zotsatira, mwa lonjezo limene linapangidwa pamenepo. Ndipo pano pali amuna awiri amene sanayambe akomanapo mu moyo, basi monga amuna awiri aja anali pamenepo. Ndipo ngati Yesu akanali yemweyo, iye akhoza kudzipereka mzimu wake ku chikhulupiriro, ndipo ine ndikhoza kudzipereka mzimu wanga ku chikhulupiriro, kwa Khristu, mwa mphatso Yauzimu ya Mzimu Woyera, ndipo tikhoza kuchita chozizwitsa chomwecho. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ndipo ndi chauzimu. Mukuti, "Ndi chozizwitsa?" Chabwino, ine ndingadziwe motani izo, ngati ine sindinayambe ndamuwona iye? Manja anga ndi awa. Ife sitinayambe takomanapo kale. Ife, pano ife taima, kwa nthawi yoyamba. Mulungu akumudziwa iye; ine sindiri.

213 Tsopano, kumbukirani, khalani mukundipempherera ine. Tsopano nthawizina mu izi—mu nthawi izi, Mzimu umakudzoza, ndipo wakhala ukuchita izo mochuluka kwambiri tsopano, mpaka zikukhala ngati . . . Chabwino, ine—ine ndikungofuna kuti inu mukhale mwabata. Mukhale molemekeza kwenikweni. Penyani. Mukhale mu pemphero.

214 Tsopano, ine ndikungofuna inu, bwana, pokhala osakudziwani inu, koma inu muli pano pa chifukwa china chimene ine sindiri kuchidziwa. Koma chirichonse chimene icho chiri, ndipo Ambuye Yesu akalola kundiuza ine chimene inu mukufuna kwa Iye, popanda inu kundiuza ine, izo zingamupange Iye basi chimene ine ndinati Iye anali, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Inu mukukhulupirira izo?

[M'bale ati, "Zedi."—Mkonzi.] Chabwino. Iye akukhulupirira izo. Ndipo tsopano omvetsera akukhulupirira izo. Ndipo Ambuye anena kuti Iye akanati adzachite izo, mu Baibulo Lake.

215 Tsopano, apa ndi pamene ine ndimapezeka mwina ndikunena Choonadi ndi Baibulo la Mulungu, kapena Baibulo lalonjeza chinachake chimene Ilo silingakhoze kuchiyimira kumbuyo, kapena ndine wachinyengo; chimodzi kapena chimzake. Mukuona? Ndiko kulondola. Muwone pamene iwe umadziyika wekha. Ine ndazichita izo pamaso pa ambiri mbiri, zikwi za anthu, otsutsa ndi onse. Koma ine ndikudziwa kuti Iye amalonjeza, ndipo Iye amasunga lonjezo Lake.

216 Ine ndikuwona Izo zikuyamba pakali pano tsopano. Ine ndikuwona anthu pokuzungulira iwe, pa nsanja, ndi kunja kwa msonkhano, ife tinalibe aliyense pozungulira. Mukuona? Alipo anthu odwala pano. Mwamsanga pamene Iwo ukuyamba, iwe ukhoza kuwumverera Iwo. Iwo ndi Mzimu Woyera. Khalani molemekeza kwenikweni tsopano, molemekeza basi tsopano, momwe ife tingakhoze kuyankhulira. Inde, bwana. Ambuye Yesu amatikonda tonse ife, pakuti ndife amuna awiri amene Iye anawafera. Ndipo nthawi yathu yoyamba kukomana. Ngati inu muli osowa, Mulungu ali wokhoza kupereka pa chosowa chimenecho, chifukwa Iye analonjeza kuti Iye akanadzatero.

217 Koma tsopano, bamboyu, ngati ali woona mu mtima wake, iye akuzindikira kuti chinachake chiri kuchitika. Iye sangakhoze kungoganiza ndendende chimene icho chiri. Koma Mngelo uja yemwe inu mumamuwona pa chithunzi, akubwera pafupi ndi pafupi kwa bamboyu, ndipo iye akuzimirira kutali ndi ine. Ndipo bamboyu akuvutika ndi vuto la mtima, ndipo iye ali ndi matenda a shuga. Ndiko kulondola. Ndizo PAKUTI UKUTERO MZIMU. Ngati izo nzoona, kwezani mmwamba dzanja lanu.

218 Tsopano, ngati ine sindinayambe ndakuwonani inu, ine ndikanadziwa motani chirichonse chokhudza inu? Njira yina, njira yomweyo imene Iye anadziwira kumeneko. Ndi kulondola uko? [M'bale ati, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.] Kodi omvetsera akukhulupirira izo? [Osonkhana ati, "Ameni."]

219 Tsopano, bwanji—bwanji osati tingotenga nthawi yathu, pang'ono pokha basi, chotero kuti inu muwone kuti sikunali kungopeka chinachake. Tiyeni titenge chinthu chinachake, ndipo tiyeni tingowona ngati Mzimu Woyera ukanati uwulule chinthu chinachake kwa ife. Tiyeni tingoyankhula kwa bambo waima apoyo, miniti yokha. Mwinamwake pali chinthu chinachake mu moyo wake, mwinamwake chinthu chinachake cholakwika ndi iye. Ine sindiri kudziwa.

220 Ine sindiri kudziwa kwenikweni chimene ine ndinanena. Ine ndikasowa kuti ndikachiwone icho pa zojambulidwa kuno, chifukwa, mukuona, ndi masomphenya, iwe umaona pamene iye

anali ali. Inde, ine ndikuziwona izo tsopano. Ndi chinachake chokhudza magazi ake. Ndi shuga. Eya, ndi matenda a shuga. Iye ali ndi matenda a shuga, ndipo izo zayambitsa vuto la mtima, chimene chayambitsa mtima wamanjenje. Iye wakhala ndi izo kwa nthawi ndithu. Ndipo iye si wochokera ku mzinda uno. Koma iye ndi wochokera ku Indiana, akuchokera ku malo pafupi ndi malo otchedwa monga Borden. Inu . . . Ine ndikuona Borden. Ndinu ochokera ku Borden. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndi zimenezo.

Ndipo pali chinachake cholakwika mu moyo wanu.

221 Pano pali chinthu china. Ine ndikuona mkazi akuwonekera pano mu masomphenya, chifukwa inu muli mu . . . Ndi akazi anu, ndipo iye akusowa machiritso ena. Ndipo iye akuvutika ndi mtundu wina wa kukhosomola. Ndi mphumu, iye ali nayo.

222 Ndipo inu muli ndi chinthu china cholakwika mu moyo wanu, chimene inu mwakhala mukuyesera kuti muchichite. Mwa chikhulupiriro, ndinu wa Chipentekoste, chifukwa, inu, ndikukuwonani inu pa msonkhano wa Chipentekoste kumene iwo akufuula ndi kuwomba manja awo. Ndipo inu mukuyesera kusiya . . . Inu mumasuta. Ndicho chimene inu mukuyesera kuti muchisiye, kusuta ndudu. Ndiko kulondola ndendende. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndicho choonadi. Sichoncho izo? Zedi, izo ziri. Mukuona? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali pano tsopano, alipo? Kodi ndinu wokonzeka kuti mulandire machiritso anu?

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

223 Ambuye Mulungu, Yemwe munamudzutsa Yesu Khristu Yemwe ali pano tsopano, bambo uyu, Ambuye, yemwe ali pano kufuna madalitso a Mulungu kuti akhale pa iye, ife tikupemphera kuti Inu mumupatse iye chokhumba cha mtima wake, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

224 Bwererani kwanu, mukazipeze izo basi momwe inu mwakhulupirira. Ndi momwe izo ziti zikakhalire. Mulungu akudalitseni inu.

225 Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mulungu Wamphamvuzonse, Yemwe analemba Baibulo ili, Yemwe Mzimu wake ulipo, akudziwa kuti ine sindinayambe ndamuwonapo bamboyu mu moyo wanga, mwachidziwikire, mpaka miniti iyi yomwe. Koma, ine ndikudziwa chinthu chimodzi, Mzimu Woyera uli pomwe pano. Ine sindiri kudziwa chimene Iye ati achite, koma ine ndikudziwa kuti Iye ali pano.

226 Kodi ndi uyu donayo? Chabwino. Kodi ndife alendo kwa wina ndi mzake? Chabwino, inu—inu—inu munandiwona ine ku misonkhano, koma ine sindikukudziwani inu. [Mlongo ati, "Ayi. Ayi."—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Chabwino. Ndiye, muli pano pa cholinga china.

227 Tsopano, mkaziyo akhoza kukhala pano . . . Iye akhoza kukhala Mkhristu; iye akhoza kusakhala. Iye akhoza kukhala wotsutsa. Ngati iye ali, ingopenyani chimene chiti chichitike. Mukuona? Ndipo ine sindikudziwa chimene iye wadzera.

228 Mayi anga akhala penapake mu nyumba muno, mkazi wachikulire. Kodi inu mungaganize kuti ine ndingayesere kuti ndimupweteke munthu wosawuka ameneyo? Inu mukuganiza kuti ndingabwere kwa iye ngati wachinyengo? Ine ndithudi sindikanatero. Ine kunali bwino kungochoka pa nsanja pano ndi kupita kwathu; ine ndalalikira kale Uthenga. Koma izo zonse si zimene zimapita ndi Uthenga. Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse. Sindikusamala chomwe dziko likunena za izo. Ife tiyenera kuima ndi izo, mulimonse. Mulungu anati tizichita izi.

229 Pokhala osakudziwani inu; ndipo, ndithudi, inu mwakhala mu msonkhano, mwinamwake mmene muli mazana ndi mazana a anthu, ine ndiribe njira ya kukudziwirani inu. Koma pano pali chithunzi tsopano cha Yohane Woyera 4, mwamuna ndi mkazi, kukomana kwa nthawi yoyamba. Ambuye wathu ndi mkazi waku Samaria akukomana kachiwiri. Tsopano iwo anayankhula. Iye anawukhudza mzimu wake, anadziwa chimene chinali cholakwika ndi iye, ndipo anamuuza iye, ndipo iye anamuzindikira Iye kuti anali Mesiya. Kodi inu mungachite chinthu chomwecho? Inu mungatero.

230 Kodi omvetsera angachite chinthu chomwecho, mkazi aliyense kunja uko? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mulole Mulungu apereke izi. Inde.

231 Mkaziyu akuvutika ndi—chikhalidwe cha manjenje. Iye wakhala nazo izo kwa nthawi yaitali, zaka zambiri mmbuyo. Ine ndikukhoza kumuwona iye panobe ali mkazi wamng'ono. Koma icho si chinthu chachikulu chimene iye akufuna kuti ine ndichipempherere. Ndi nyamakazi imene yamulumalitsa iye. Ndi chimene inu mukufuna ine kuti ndichipempherere.

Tsopano kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

232 Tiyeni tiyankhule kwa iye mopitiriza pang'ono. Mulole Mzimu Woyera upereke izi. Mkaziyu ali makamaka—wamayankhulidwe akwina. Dzina lake ndi Hanson. Ndi zoona. Wachi Norway kapena wachi Swedish, iye. Sindinu wochokera ku mzinda uno. Ndinu ochokera ku malo otchedwa Canton. Ndipo uko ndi ku dziko lalikulu kumene kuli tirigu wambiri. Ndipo ndi ku Minnesota. Ndi kumene inu mukuchokera. Izo nzoona. Tsopano bwererani kwanu; inu mwachiritsidwa. Yesu Khristu wakupangani inu wabwino. Kawauzeni anthu zinthu zabwino zimene Ambuye achita kwa inu.

233 Ine ndiri kulingalira kuti ife tiri alendo kwa wina ndi mzake. [Mlongo ati, "Inde. Ine ndakhala ndiri mu misonkhano, koma inu

simuli kundidziwa ine."—Mkonzi.] Ine sindikukudziwani inu. Ayi, mayi. Koma Ambuye akukudziwani inu. Inu muli pano pa cholinga china. Ine sindiri kuchidziwa. Koma ngati Ambuye Yesu ati awulule kwa ine chimene inu mwadzera pano, inu mudziwa ngati izo ziri choonadi. Ngati ine ndikanabwera pano ndi kudzati, "Inu mukudwala, mkazi." Zedi, inu muli kuima pa mzere wa pemphero, izo zikusonyeza . . . [Malo osajambulidwa pa tepi.]

234 Kupimidwa kwanu kukusonyeza kuti inu muli ndi chinachake cholakwika ndi chiwindi. Iye anati izo zinali kuwuma kwa chiwindi. Ndiko kulondola. Ndingoyankhula kwa iye miniti. Basi . . . Kodi inu mukukhulupirira kuti Ambuye Yesu, yemwe anayankhula kwa mkazi pa chitsime, ali yemweyo lero? [Mlongo ati, "Inde."—Mkonzi.] Inu mukutero? Muli, mukuwoneka ngati muli ndi mzimu wabwino. Sindinu wochokera kuno. Inu mukuchokera kummawa, mukuchokera ku Ohio. Ndiko kulondola. Dayton, Ohio, kubwera kuno. ["Ndiko kulondola."] Ndiko kulondola. Ine ndikuona . . .

235 Inu mukumupempherera winawake. Uyo ndi mnyamata. Iye ali ndi vuto la mtima. Iye ali ndi zironda, nayenso, mnyamata wokhala ngati wamanjenje. Ndiko kulondola. Ndipo inu mukupempherera moyo wake, chifukwa iye ndi wosapulumutsidwa. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Izo ndi zoona. Sichoncho izo? ["Mwana wanga."] Inu mwachiritsidwa. Bwererani. Kamuuzeni iye, akhale wolimba mtima bwino. Yesu Khristu . . .

236 Sindiri kukudziwani inu, dona, sindiri kukudziwani inu. Mulungu akukudziwani inu. Ngati Mulungu ati andiuze ine lomwe liri vuto lanu, inu mundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Ndikutsimikiziritsa Iyeyekha. Mukuona, chimene ine ndikufuna kuti ndichite ndi kuwatenga anthu awa, amene akubwera mu mzere wa pemphero, kuti awone kuti Iye ali pano.

237 Chinachake chinachitika mu msonkhano. Pali akazi awiri aima apowo atavala, onse, magalasi. Winawake wamugwira Iye, ndi kumverera kwa zowawa zawo. Ine ndikukhoza kungomuwona mkaziyo, chimene . . . Vuto lanu la khutu, ilo lapita tsopano. Tayang'anani pa donayo, momwe iye akuwonekera mochuluka monga uyu apa. Iwo anali ataima apo. Ine ndimakhoza kuwaona iwo. Koma mmodzi anali akuchita *izi;* ndipo panalibe kanthu kotero kwa mmodzi *uyu*.

238 Chifukwa cha izo chiri, mkazi uyu akuimira munthu winawake. Ndiko kulondola. Ndipo mkazi uyo ndi woyandikana naye wanu. Ndipo iye ali ndi nyamakazi. Ndipo inu mukumuimira iye. Ndipo ine ndikukuwonani inu mukumupempherera iye, chifukwa iye ndi wosapulumutsidwa. Ndipo inu mukumupempherera iye. Ndicho chinthu

champhamvu. Kaikeni mpango uwo pa iye, umene inu muli nawo mdzanja lanu. Kamuuzeni iye kuti asati akaikire, ndi kuti akapereke moyo wake kwa Khristu, ndipo nyamakazi yake imuchokera iye.

239 [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]. . .mukumulirira, mlongo? Inu mukumukhulupirira Mulungu? Inu mukukhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine chimene inu muli kulirira, ndi chimene chokhumba chanu chiri? Ngati inu mukukhulupirira izo, kwezani mmwamba dzanja lanu. Kodi inu mukukhulupirira kuti chotupa icho chimusiya iye? Ngati inu muti mukhulupirire izo, icho chipita. Ingokhalani nacho chikhulupiriro. Musati mukaikire basi.

240 Inu muli bwanji? Ndikuganiza ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ambuye Yesu akutidziwa tonse ife. Ndinu mkazi wamng'ono wamphamvu. Koma inu simuli pano chifukwa cha inumwini. Ine ndikuwona chipatala chikutulukira, kama. Ndi amayi anu amene inu mukuwapempherera, ndipo iye ali ndi mthunzi wa imfa. Iye akuvutika ndi ndulu, zotupa. Ndipo iye ali ndi khansala, naponso, mthunzi wakuda wa khansala. Tengani mpango umenewo, umene inu mukulirilapo, mukawuyike iwo pa iye. Ndipo mukaitanire pa Dzina la Ambuye, ndipo musati mukaikire. Ngati inu simukaikira, Mulungu akamuchotsapo iye apo ndi kumukhalitsa bwino iye. Musati mukaikire tsopano. Pitani mu Dzina la Ambuye, ndipo kakhulupirireni.

241 Kodi inu mukukhutitsidwa kuti Khristu alimoyo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

242 [M'bale Branham akuimikira—Mkonzi.] Pali chinachake cholondola. . . O, ndi mkazi wakhala kumbuyo komwe kuseri uko, mu mpando uwo. Iye akuvutika ndi mitu. Ndipo iye wakhala akupemphera kwa Ambuye, uko, akuyesera kuti azimusamalira mwana uyo. Iye anakumvani inu, mlongo. Izo zonse zatha tsopano. Ingoimirirani pa mapazi anu, kuti mumupatse Mulungu matamando chifukwa cha izo, dona. Ingomupatsani Mulungu matamando chifukwa cha izo. Mukuona?

243 Kodi iye anagwira chiyani? Iye sanandigwire ine konse. Koma iye anamugwira Wansembe Wamkulu uja. Ine sindiri kumudziwa mkaziyu. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye, mu moyo wanga. Koma Mulungu wamuchiza iye apo basi. Kodi izo zikumupanga Yesu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Zedi, izo zikutero. Ngati inu mungakhoze kukhulupirira! Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira.

244 Iwo ukugunda omvetsera, munthu wina akupemphera. Mwaona, izo zimatengera pamene mphamvu ikuchulukira, kumene kuli Mzimu. Ine ndikhoza kutsatira kokha ndi kunena

monga Iye akunenera; ine sindimadziwa. O, ndi mkazi yemwe wavala magalasi ake, akulira. Chifukwa chimene iye anali kulira, chifukwa Mzimu uli pa iye. Apo Iwo uli. Vuto la matumbo lija limene inu mwakhala mukuvutika nalo; khalani ndi chikhulupiriro, izo zikusiyani inu ndipo sizidzabwerera konse. Ine sindikumudziwa mkaziyo. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye. Iye sanandikhudze ine konse. Iye wamukhudza Wansembe Wamkulu.

Ngati inu mungakhoze kukhulupirira!

245 Iwo unamugunda mkazi wina. Ine ndikufuna wina aliyense yemwe akufuna kutero, yang'anani kuno. Tayang'anani pa mkazi akulirayu; tayang'anani pa mkazi winayo yemwe wakhala bwinobwino; tayang'anani pa mkazi winayo wapafupi ndi iye, akulira. Iye anali ndi vuto la mtima, dona wamng'ono wakhala pomwepoyo, akuyang'ana pa ine ndi lanu. . .Eya. Ndiko kulondola. Inu munali ndi vuto la mtima. Sichoncho inu? Ilo lakuchokerani inu. Chikhulupiriro chanu chinayatsa moto ndi Mulungu, ndipo inu munamugwira Iye.

O, izi ndi zodabwitsa!

[M'bale Branham akuimikira kwa mphindi makumi awiri ndi zisanu—Mkonzi.]

246 Muikumuwona dona wakhala apo pomweyo ndi mutu wake chowerama, akupemphera? Mkazi wa mutu wa imvi, mlendo kwa ine, atakhala apo. Inde. Inu munatembenuka mozungulira, kumayang'ana pa uyo. Iye ali ndi vuto la ndulu. Iye wakhala akupemphera kuti Mulungu achichotse icho kwa iye. Ndipo inu munali kupemphera pamenepo, "Ambuye, muloleni iye andiyitane ine." Ndiko kulondola. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ine ndinadziwa bwanji pemphero lanu? Izo zachoka kwa inu. Chikhulupiriro chanu chakuchizani inu. Pitani kwanu ndipo mukakhale bwino.

247 Kodi inu mukukhulupirira? Ngati inu mungakhoze kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheka. Koma inu muyenera kuti mukhulupirire.

248 Ukusunthabe mu boma limenelo, la yemwe wakhala mkati *mmenemo*. Pomwe *pano,* wachiwiri kuchokera kumapeto, kuthamanga kwambiri kwa magazi. Ngati inu muti mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, mlongo, izo zatha. Kodi inu mukumukhulupirira Mulungu, kumutenga Iye pa Mawu Ake? Chabwino. Kwezani dzanja lanu mmwamba. Ndicho chimene inu munali kuchipempherera, "Ambuye, muloleni iye andiyitane ine potsatira, ndi kuthamanga kwambiri kwa magazi uku." Ine ndine mlendo kwa inu. Ngati izo ziri zolondola, gwedezani dzanja lanu. Chabwino. Izo zachoka kwa inu. Pitani kwanu ndipo kakhaleni bwino.

249 Inu mukuona chimene icho chiri? Ndi chikhulupiriro. Ndipo ngati inu mungakhoze kuzikhulupirira izo! Kodi inu

mukukhulupirira? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Onani, anthu awo kunja uko, opanda makadi apemphero kapena kanthu. Kodi inu muli okonzeka kuti mukhulupirire? Kodi umo ndi momwe Ambuye Yesu ankachitira pamene Iye anali pa dziko lapansi?

250 Pano, kodi uyu—kodi ndi mmodzi uyu, bambo akubwera? Chabwino. Inu simukudziwa chimene izo zimachita kwa inu nonse. Kwa Branham Tabernacle, tsopano tangoyang'ana kuno pamwamba manja. Mwaona? Inu mukudziwa ine sindimachita chotero. Ndi chiyani icho? Mzimu wa Ambuye. Iwo ukudzoza.

251 Anthu ambiri samamvetsa chomwe kudzoza kumatanthauza. Iwo amaganiza kuti iko kumatanthauza kufuula. Icho ndi chisangalalo. Mphamvu imabwera moopsya. Mukuona? Icho ndi chisangalalo cha Ambuye. Iyi ndi Mphamvu ya Ambuye; kumuchiza iye, kumupanga iye wabwino. Penyani chimene Iye anachita kwa msungwana wamng'ono atakhala usiku wina, wolumala; kwa munthu wakhungu; kwa ena, kupyola paliponse.

252 Inu muli bwanji, bwana? Ine ndikulingalira ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ife sitiri kudziwana wina ndi mzake. Ine sindikukudziwani inu, ndipo inu simuli kundidziwa ine. Ngati izo ziri zolondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino, nthawi yathu yoyamba kukomana. Molemekeza tsopano. Pano pali mwamuna, ndipo iye ndi ine. . . wamng'ono kwambiri kuposa ine, ndi manja athu ali mmwamba, kwa wina ndi mzake, pamaso pa Mulungu, kuti iyi ndi nthawi yathu yoyamba kukomana. Yesu akumudziwa bamboyu. Ndipo payenera kukhala pali chinachake cholakwika; iye kuima pamenepo. Ine sindikuchidziwa.

253 Koma ngati ine ndanena choonadi, chimene Mulungu watsimikizira mwa mboni zochuluka, kuti ine ndakuuzani inu choonadi, kuti, "ndi mikwingwirima Yake inu munachiritsidwa." Iyo ndi tensi yakale. Inu muyenera kupeza chikhulupiriro cholimba icho, kuti mukwere pamwamba pa zinthu izi.

254 Tayang'anani pa khansala ikuchoka pano usikuuno! Tsopano inu mungopenya maumboni amene akubwera kuchokera pamenepo, mithunzi yakuda ya imfa iyo. Dokotala wanu wokondeka akhoza kuyesa, zonse zimene iye akanakhoza kuchita, kuti apulumutse moyo wanu. Koma pamene Mulungu anena chirichonse, ndi zimenezo. Ndipo izo sizinali ine. Ine ndiribe kanthu kochita ndi izo.

255 Tsopano alipo pafupi mazana awiri pano oti apemphereredwe. Ine ndikufuna kuti ndipume miniti yokha tsopano. Ndiyeno ife tidzangoyamba kumawapempherera anthu, kuwabweretsa iwo pano; osati kuwadutsitsa iwo kupyola mu mzere, koma nditaima pano kumawapempherera iwo. Ine

ndikufuna kuti ndimupempherere aliyense yemwe akufuna kuti apemphereredwe.

256 Koma mwa omvetsera onse, ndi iwo amene ali pa nsanja, ine ndikufuna inu kuti muzindikire kuti Yesu Khristu ali pano. Kodi inu nonse muli kuzindikira zimenezo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Aliyense akuzindikira izo. ["Ameni."]

257 Tsopano, kuti izo zikhoze kukhala zokhazikika kwa nthawizonse mu malingaliro anu. Bambo uyu ndi ine, pano ndi manja athu mmwamba kwa Mulungu, nthawi yathu yoyamba kukomana. Ngati Iye ati ayankhule chinsinsi cha mtima wake, monga momwe Iye anachitira kwa mkazi wa pa chitsime, kapena kwa Filipo, kapena mpaka kulikonse mpaka kupyola mu utumiki Wake, ngati Iye ati achite izo, kodi izo zitsimikizira kwa inu nonse, kuti ndi mwamtheradi Iye, Ambuye Yesu? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.]

258 Kodi zitero kwa inu, bwana? [M'bale ati, "Inde, bwana."—Mkonzi.] Ine ndiribe njira, ndiribe lingaliro chomwe vuto lanu liri. Ine sindikudziwa kaya ndinu wochimwa kapena Mkhristu. Ine sindikanakhoza kukuuzani inu. Iye amatero; Mulungu amatero. Koma ine sindingakhoze kukuuzani inu. Koma ngati Iye ati andiuze ine. . . Koma inu ndinu Mkhristu. ["Inde."] Chifukwa, mwamsanga pamene mzimu wanu ukugwira kudzoza kwa Mzimu uwu umene uli pa ine, iwo ukuulandira Iwo, chotero ine ndikudziwa ndinu Mkhristu.

259 Ndipo inu muli pansi pa mthunzi wakuya. Ndi chinachake cholakwika ndi magazi. Ndipo inu mwakhala muli kwa madokotala. Ndipo iwo akufuna kuti apange opareshoni, ndipo opareshoni imeneyo ili, ine ndikuwamva iwo, ndipo madokotala awiri akufunsana wina ndi mzake, ndipo iwo akufuna kuti atenge chiwalo kuchokera mu thupi lanu, chimene chimatchedwa ndulu. Ndiko kulondola. [M'bale ati "Inde."—Mkonzi.]

260 Ndipo inu simuli ochokera mu mzinda uno, koma ndinu ochokera ku mzinda waukulu kumene kuli masukulu aakulu a mtundu wina wa chipembedzo. Ndi ku Wheaton. Ndipo dzina lanu ndi Karl Rhodes, Rhodes, chinachake chonga Karl Rhodes. Chabwino, bwana. Ngati inu muti mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kubwerera kunyumba kwanu, ndipo Mulungu akusiyirani moyo wanu. Kodi inu mukukhulupirira izo? [M'bale ati, "Ine ndikukhulupirira izo."—Mkonzi.]

Tiyeni ife tipemphere.

261 Ambuye Yesu, ine tsopano ndikuponyera kutali choyipa ichi kuchokera kwa m'bale wanga. Ndipo mu Dzina la Yesu Khristu, mulole iye akhale moyo kwa ulemerero wa Mulungu. Ameni.

Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Pa ulendo wanu, mukusangalala!

262 Ndi angati akukhulupirira tsopano ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana Ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

Tsopano, kodi ndiwo onse omwe ati apemphereredwe? Chabwino.

263 Chabwino, vuto lanu la nsana linakusiyani inu pamene inu munali mutakhala apo, kotero inu mukhoza kupita pa ulendo wanu, ndipo muzisangalala ngati inu mukufuna kutero. Ndipo muzingopitirira, kumati, “Ndikuthokoza Ambuye wabwino!”

264 Inu mupite mukadye chakudya chanu chamadzulo. Vuto lanu la mmimba lakusiyani inu, mukubwera mu mzere, kotero inu mukhoza kupita ndi kukakhala ndi ulendo wanu, inunso. Mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse.

265 Nyamakazi yanu sikuvutitsani inu, ngati inu muti mukhulupirire izo. Ingomapitirirani choncho, mukusangalala ndi kumatamanda Mulungu, ngati inu mungatero, m’bale. Chabwino. Chabwino.

266 Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi angati akumukhulupirira Mulungu? [“Ameni.”] Tsopano ine ndikuti ndingoponda apa mphindi yokha.

Munthu Woitanidwa Ndi Mulungu CHA58-1005E
(God-Called Man)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu usiku, pa Okotobala 5, 1958, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1999 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1999 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org